


File Copy

**KUYANG'ANA MTSOGOLO NDI
CIYEMBEKEZO**




**"HIS LIFE IS THE LIGHT THAT SHINES
THROUGH THE DARKNESS — AND
THE DARKNESS CAN NEVER
EXTINGUISH IT." JH 1:5 (L.B.)**

**Published and Printed by
BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia**

Cover Design By J.W. Tembo

—————
—————
—————

**KUYANG'ANA MTSOGOLO NDI
CIYEMBEKEZO**



"HIS LIFE IS THE LIGHT THAT SHINES
THROUGH THE DARKNESS — AND
THE DARKNESS CAN NEVER
EXTINGUISH IT." *JN. 1:5 (L.B.)*

—————
—————

KUYANG'ANA MTSOGOLO NDI CIYEMBEKEZO

Published and Printed by
BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

Copyright 1989
BAPTIST PUBLISHING HOUSE
All Rights Reserved
Printed with Permission
of Baptist International Publications Services

Nenani: Ndi capafupi kukhala kazembe wa Kristu ngati tilankhula za iye. Ndi capafupi kunena zomwe Kristu anaticitira ife. Tiyenera kukumbukira kunena za Kristu kwa aliyense amene takomana naye.”

Tsilizani: “Ngati tifuna kuti tiyanjanitse dziko wa Kristu, tiyenera kukhala otanganidwa masiku onse. Pamene tilankhula dzina la Kristu tinene zomwe aticitira, tili kubweretsa dziko kwa iye pamodzi. Tiri mbali ya kufalitsa uthenga mu dziko. Nchito yathu siinathe kufikira yense atamva uthenga umenewu wa Yesu.”

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero, kupempha ophunzira anu kuti akhale ndi mphamvu za kulalikira za Yesu.

ndipo ophunzira anu amasulire: Salmo 18:49; Deutronomo 32:43; Salmo 117:1 ndi Yesaya 11:1. Werengani Aroma 15:13. Nenani: “Ndime ili ipatsa mutu wa nkhani ya maphunziro onse-ciyembekezo. Mulungu wathu ndi Mulungu wa Ciyembekezo. Timapuma mu ciyembekezo comwe tipeza mwa iye.”

Werengani ndime la 14. Nenani: “Anthu aganiza kuti Paulo anali munthu ouma mtima, koma ndime ili ionetsa kuti anali ofatsa. Iye anali akalibe kufikako ku mpingo wa ku Aroma, koma anadziwa kuti Aroma anali odzala ndi nchito zabwino ndiponso omwe anakhoza kuphunzitsa wina ndi mnzace. Pena Priskila ndi Aquila ndiwo anampatsa nkhani yabwino iyi.”

Nenani: Mu ndime la 15 Paulo alikupepesa kwa Aroma cifukwa ca kalembedwe kace. Iye ananena kuti anagolembe ku zinthu zina cabe cifukwa zina sizinafunike kulangizidwa.”

Werengani ndime la 16-21. Nenani: “Cioneka monga kuti Paulo anali kunyadila nchito yace. Koma anali kunyadila mphamvu ya Mulungu kupambana mphamvu yace. Paulo anaika malire pa nchito yace. Palibe ndime ina imene isiya izi, koma osati macitidwe onse a Paulo analembedwa mu Macitidwe. Iye anacitadi zomwe ananena kuti adzacita.”

Pitilizani: “Paulo anafunadi kuti uthenga utengedwe ku mitundu iliyonse kuti aliyense amve nkhani yabwino yotere. Pena ndilo tanthauzo la ndime zimenezi.”

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Ndime lomaliza la (21) inacokera ku Yesaya 52:15. Ndime ili inena za kudabwa kwa mitundu pamene inamva kuti Kristu anabwera monga kapolo wotsautsidwa. Werengani ndime imeneyi. Nenani: Cifuno ca Paulo cinali cakuti onse amuone iye amene sanamuone (Yesu) ndipo iwo adzakhoza kumvetsetsa zonse zimene anafunika kudziwa za iye.”

Pitilizani: “Ndife akazembe a Kristu masiku ano. Kazembe sanena za iye yekha kapena mau ace. Iye amanena za maganizo a dziko lomwe linamutuma. Tiyenera kunena maganizo ndi kacitidwe ka Mulungu yemwe anaitituma ndikupita ku malo kumene afuna kuti tipite.”

ZA M’KATIMU

MUTU	TSAMBA
1. Nanga Ngati Zobvuta Zibwera?	3
2. Kukomana ndi Kusinthidwa	10
3. Kusunga Cikhulupiriro	17
4. Kusungidwa ndi Cikhulupiriro	26
5. Cofunikira Cathu Kuti Tiyanjantsidwe	33
6. Kuyanjanitsidwa Kupyolera mwa Yesu Kristu ...	39
7. Amoyo mwa Kristu	47
8. Ufulu mwa Kristu	54
9. Kusungidwa mu Cikondi ca Mulungu	60
10. Amodzi Pansi pa Mulungu	67
11. Umoyo wa Cijanjanitso	73
12. Kuyenda mu Cikondi	80
13. Nchito Yathu ya Cijanjanitso	87

Ndime la 16 itiuza kuti Paulo anali mtumwi wa nchito ya Mulungu. Anatanthauza kuti anasiya zonse kuti acite zimene Mulungu anamuitanila kwa Ahelene.

Ndime la 17 Paulo anena kuti anali ndi colinga cakukhala onyadira nchito ya Mulungu. Uku sikunali kuzinyadila. Uku kunali kunyada kumene Mulungu acita kwa iye. Ndime la 18 inena za cikondwerero cimene Paulo ndi cakuti anali ndi danga lakucita umboni kwa Ahelene.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Nenani: “Cimanenedwa kuti Mulungu alibe manja koma manja athu. Tiyenera kucita zimene Mulungu afuna kuti zicitidwe. Mulungu alibe mau koma mau athu. Tiyenera kunena zomwe afuna kuti zinedwe.”

Pitilizani: “Ndi cabwino kuganiza kuti tikhoza kucita nchito ya Mulungu. Koma ndi angati mwa ife omwe ali ozipereka? Ndi angati mwa ife amene angasiye nyumba zao kapena midzi yao ndi kupita kukapereka uthenga ku dela lina? Ndi angati mwa ife amene angalole manja athu kuti atsogoleledwe ndi kuti athandize odwala ndi osauka?”

Pitilizani: “Timanena kuti tidzapita kumene Mulungu afuna kuti tipite, tidzanena zimene Mulungu afuna kuti tinene. Mulungu afuna kuzipereka koono.”

KUMASULIRA

Ophunzira anu atsegule mabuku ao ku Aroma 15:8. Wina awerenge ndime 8-13.

Funsani: “Kodi muganiza kuti Paulo anatanthauza ciani kuti Kristu anakhala kapolo kwa a mdulidwe kuonetsa kukhulupirika kwa Mulungu?” Lolani kalasi lanu alankhuzane kuwathandiza kudziwa kuti Kristu anakhala mu Yuda wokwanira ngakhale mu mwambo wonse. Nenani: “Pamene aneneri a Mulungu ananena mu malo ace, anali kunena mau a Mulungu. Pamene Yesu anabwera, anaonetsa kuti aneneri amenewa ananena za mtsogola za Mesiya.”

Nenani: Ndime la 9-12 ndi ndime za mu Cipangano Cakale zomwe zinena kuti Kristu anabwerera Ayuda ndi Ahelene. Tiyeni tiwerenge ndime izi. “Werengani ndime zonse izi

MUTU 13
KWA MPHUNZITSI

COLINGA: Ndifuna ophunzira anga kuzindikira kuti ali ndi mbali ya kufalitsa uthenga.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA: Coko kapena pepala lalikulu.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Aroma 15:8-13 itiuzanso kuti Kristu anabwerera anthu onse.

Ndime la 8 “Kristu anakhala kapolo wa amdulidwe kuonetsa kukhulupirika kwa Mulungu.” Tanthauzo ndi lakuti Kristu anakwaniritsa malamulo onse a Ayuda kuonetsa kuti Mesiya ananenedwa, ndiponso kuonetsa kuti Mulungu ananena coona.

Ndime la 9-12 ndi ndime za m’Cipangano Cakale kuti Kristu anabwera koyamba kwa Ayuda, koma kuti anabweranso kwa Ahelene naonso. Ndime izi ndi : Salmo 18:49, Deutronomo 32:43, Salmo 117:1 ndi Yesaya 11:1.

Ndime la 13 ili ndi mau akuti “Mulungu wa ciyembekezo” imene ipatsa mutu wa kalata. Ngati tiri ndi cikhulupiriro, tidzakhala ndi “Cimwemwe” ndi “Mtendere” ndipo tidzakhala mu ciyembekezo.”

Mu ndime la 14 tiwerenga mau a cisomo a Paulo. Paulo ananena zabwino kwa Aroma omwe sanali atawaona kuti anali a nchito zabwino ndiponso anzeru. Ananenanso kuti analangizana wina ndi mnzace. Apa tiyenera kudziwa kuti mpingo wa ku Aroma unayamba caka coyamba Yesu atauka kwa akufa, ndi kuti unapitiliza kwa zaka 30 kopanda utsogoleri wa mtumwi. Ndiye kuti cinatengela Petro ndi Yohane zaka 30 Yesu atauka kuti iwo afike ku Rome.

Pakupepesa ku mau olimba omwe Paulo anali atawalembela, Paulo anena mu ndime la 15 kuti anangolembe mitu zokha zokha. Mu mau ena sanayese kuwalangiza mu zinthu zonse koma mu zinthu zina.

MUTU 1
NANGA NGATI ZOBVUTA ZIBWERA?

COLINGA: Phunziro iyi idzandithandiza kudziwa kuti monga Mkristu ndidzakomana ndi nthawi zobvuta, koma Mulungu nthawi zonse alipo kutithandiza.

MAU OYAMBA: Habakuku 1-3

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Habakuku. 1:2-5, 12-13, 2:1-4

MAU APAMTIMA: “*Penyani mwa amitundu, penyetsetsani, nimudabwe kwakukuru, pakuti ndicita nchito masiku ano, imene simudzabvomera cinkana akufotokozerani.*” Habakuku 1:5

Ku masabata otsatira, tidzaphunzira za mbiri ya Israyeli asanatengedwe ku ukapolo ndiponso atatengedwa. Anthu a ci Hebri anali olimba mu mzimu comwe cinawathandiza mu nthawi yomwe dziko itamwalira. Pa kuphunzira ndime izi, tidzapeza zofunikira za uzimu za Israyeli. Momwe zofunikira izi zinathandizira ana a Israyeli zikhoza kutithandizanso mu nthawi ya mabvuto.

Nanga ngati zobvuta zibwera kwa inu? Nthawi zobvuta nthawi zina zimabwera kwa anthu ena. Anthu onse amabvutika mu umoyo. Pamene mazunzo apitilira, ena amagonjera. Ndicofunikira kupilira, kukhala olimba pamene mabvuto abwera mu umoyo wanu wa Cikristu.

Mu masiku ano kuli anthu omwe ali kupeza mabvuto monga ya Habakuku. Ganizirani munthu monga Habakuku, ali kunena kuti akonda Kristu, ali ndi mkazi ndiponso ana onsewa aphedwa mu ngozi ya galimoto! Iye sanamvetsetse. Pamene nthawi yotere ibwera, tiyenera kukhala olimba ndi kuyembekezera pa Mulungu. Maiko naonso amakomana ndi nthawi zobvuta. Habakuku anaona dziko lace lilikufoka. Iye anabvutika pamene Yuda anagwa, koma sanaleke. Iye anapitilizabe kukhulupirira Mulungu mu nthawi ya mabvuto. Nkhani ya cikhulupiriro ca Habakuku inenedwa mu Buku la Habakuku. Werengani za iye mu buku lanu. Kodi cikhulupiriro cace cinamthandiza bwanji mu nthawi ya mabvuto? Werengani Habakuku 1:2-5, 12-13, 2:1-4.

MAFUNSO OBVUTISA

Tidzapeza mafunso amodzi-modzi omwe anakomana ndi Habakuku pamodzi ndi anthu ace. Nthawi inali itabvuta mu Yuda pamene Habakuku anakhala ndi maso-mphenya. Werengani 2 Mafumu 23:32 za zinthu zoipitsitsa zomwe mafumu anacita. Iwo sanamvere zomwe aneneri ananena. (Onani Yereimiya 7) Iye anaganiza kuti Mulungu sanalenge aneneri oipa.

Mneneri anaganizira pamene Mulungu akanabwera kupulumutsa Yuda kwa zoipa, ndi macitidwe oipa. Izi zinali bodza, kupembedza mafano, kuba ndi kutsausa anthu. Habakuku anaganizira cifukwa cace comwe Mulungu salekeza zonse izi kutha. Iye anadandaulira Mulungu. Iye anafuna kudziwa nthawi yomwe mabvuto adzatha. (Ndime 3-4). Habakuku anaganiza kuti anthu oipa sanafunike kupangitsa anthu ace kubvutika.

Mulungu anali atabvumbulutsa Habakuku kuti anthu aku babulo mtundu woipa udzagwiritsidwa nchito kulanga Yuda. Koma Habakuku sanamvetsetse ici. “Kodi Mulungu angagwiritse bwanji nchito mtundu woipa kulanga mtundu wabwino.” Iye anaganizanso ngati cinali cotheka kukhala cete pamene mtundu unali kuononga Yuda.

KUMVERERA YANKHO YA MULUNGU

Habakuku anapitiliza kufunsa mafunso. (Onani ndime ya 14-17) Anayesa kupeza mayankho. Iye anayembekezera yankho ya Mulungu. Iye sanasiye. Ndipo Mulungu anapereka yankho, (Onani ndime 2). Mulungu ayankha anthu onse. Lembani yankho mu malemba akulu akulu pa mwala kapena pa bolodi kuti anthu anu awerenge pamene ali kuthawa adani ao a Chalediya. “Ambuye anatero. Anauzanso Habakuku kuti zinthu izi sizizacitika tsopano. (Onani ndime 3) Mulungu adzathandiza anthu ace pa nthawi yace. Mulungu anauza Habakuku kukhala oledza mtima. “Usalephere Mulungu anatero. Zinthu zidzayenda monga ndazikonzera.” Mulungu anabvumbulutsira Habakuku zomwe anaganiza pa Achalediya. Iwo anali onyada. Anaika cikhulupiriro mwa iwo okha. Koma adzagwa monga Mulungu ananenera. Werengani Mau a Mulungu a ciweruzo ca mu babulo, (Habakuku 2:6-10). Penyetsetsani ndime 4 kuti mphamvu yoipa idzaziononga iyo yokha. Mulungu

OPANGA MTENDERE

Akazembe amapanga mtendere. Paulo nayenso anapanga mtendere. Anathandiza anthu kudziwa Mulungu. Pamene anthu akhala mu cikondi ca Mulungu, adzakhala a mtendere.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Mphamvu ya Mulungu ikhoza kupita mu dziko lonse. Mukhoza kuuza ena zomwe Yesu akucitirani. Mungathandize odwala. Mungaphunzitse ena za Ambuye.

Kumbukirani kuti nanunso mufunika kuthandiza ena za kukhala mu cikondi. Mufunika kuthandiza ena kukhala a mtendere mu mtima mwao. Mudzacita ciani lero kutenga nkhani ya cijanjanitso kwa wina?

CITSANZO CA KRISTU

Yesu ndi citsanzo cathu cabwino. Iye anali munthu wolungama. Tiyenera kuyesa kukhala monga Mbuye wathu.

Tilondola citsanzo ca Yesu pamene tithandiza ofoka. Tilandirane wina ndi mnzace mu cikondi ca Cikristu. Ndipo tidzabweretsa ulemerero kwa Mulungu.

CITSANZO CA PAULO

Umoyo wa Paulo naonso ndi wabwino. Sunalingane ndi Yesu. Koma umoyo wace ukhoza kutithandiza kumvetsetsa momwe tikhoza kukhalira ndi Mulungu. Paulo analembela Akristu a ku Roma kuti akonde abale ao ofoka. Paulo anali wolimba, koma anathandiza ofoka. Analondola citsanzo ca Yesu.

Paulo anadziwa kuti Akristu ambiri mu Roma anali olimba ndipo anakhoza kuphunzitsa ena. Koma anadziwa kuti akanaphunzira zambiri. Analembela kwa Akristu amene anamvetsetsa Mulungu bwino. Mu ndime 15-21, Paulo analemba za maitanidwe ace. Mulungu anamuitana kulalikila uthenga wabwino wa cipulumutso kwa Ahelene.

Mulungu anagwiritsa nchito Paulo kuthandiza Ahelene pa kakhalidwe kabwino. Anaphunzira momwe angakhalire abwenzi ndi Mulungu. Paulo anayenda ku malo ambiri kulalikira kwa Ahelene ndipo iwo anavetsetsa. Anadziwa za cikondi ca Mulungu. Anadziwa kukonda Mulungu. Paulo anafuna kukhala mtumwi wa ku maiko ena. Anafuna kulalikila kwa ena amene sanamvere uthenga. Anafuna kukhala woyamba kukza anthu amenewo za Yesu. Sanafune kumanga pa madziko a ena. (Onani ndime 2) Paulo anadziwa kuti ambiri anali asanamve za Yesu. Anafuna kupita kumeneko kukalalikira. Anali kufuna-funa omwe sanadziwe Yesu. Anafuna kuti ambiri adziwe Yesu monga Mpulumutsi.

Paulo anali kazembe wa Kristu. Kazembe anali kuimilira dziko lace mu dziko lina. Paulo analankhula za Mulungu. Anabweretsa uthenga wabwino ku dziko.

Paulo anatiikila citsanzo cathu. Anationetsa kukondana. Anationetsa kugawa cikondi ca Mulungu ndi iwo amene sadziwa.

anaitana Habakuku kukhala umoyo wokhulupirika. Iye sanafunike kufunsa macitidwe a Mulungu. Anafunika kukhulupirira Mulungu. Mneneri anadabwa cifukwa cace Yuda anacimwa motere. Koma iyi siinali bvuto kwa Mulungu. Ngakhale tsopano Mulungu apitiridza kukwaniritsa dziko. Habakuku tsopano anabwera ndi maso-mphenya ndiponso ndi uthenga. Tsopano analibe mantha ndi a babulo. Anakhulupirira Mulungu ngakhale nthawi zobvuta zitabwera. Mulungu anayankha Habakuku.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE:

Inunso, mumakomana ndi nthawi zobvuta. Mukhoza kukhala ndi mafunso obvutitsa mu umoyo wanu. Kodi mufuna kugonjera? Muike cikhulupiriro canu mu ubwino wa Mulungu ndi colinga cace pa umoyo wanu. Phunzirani kunena kuti “Yehova Mulungu ndi mphamvu yanga, ndipo adzandibweretsa mwa ubwino ku maphiri.”

**MUTU 1
KWA MPHUNZITSI**

COLINGA: Ndifuna ophunzira anga kusamira pa Mulungu ku mayankho a mabvuto a umoyo.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Mapensulo ndi mapepala.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA:

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Buku ya Habakuku ndi yabwino. Habakuku ndi iye yekha mneneri yemwe aimilira a Israyeli kwa Mulungu. Aneneri onse anaimilira Mulungu kwa Israyeli. Tanthauzo apa ndi lakuti, Habakuku analankhula kwa Mulungu. Anafunsa Mulungu mafunso ambiri ndipo Mulungu anali kuyankha.

Zinthu zomwe ziri mu buku ndi zomwe zinacitika ndi mafumu ocimwa a Yuda. Cioneka monga kuti Mulungu analola mafumu amenewa kukhala monga anafunira. Cimo linali ponse ponse mu dziko. Habakuku anaona zonse izi ndipo anafunsa Mulungu comwe analolela izi kucitika.

Mulungu anayankha kuti analola mtundu wocimwa (Anthu a ku Babulo) kugonjetsa Yuda monga cilango cao. Ananena kuti potsiliza iye adzaononga a ku Babulo cifukwa ca ici.

Mulungu anauza Habakuku kuti zinthu zonse zinali m'manja ace, ngakhale mitundu ya kunja.

Mulungu anakumbutsanso Habakuku kuti zonse izi zinali ndi nthawi yace.

Habakuku 1:2-5 ndi kulankhuzana pakati pa Habakuku ndi Mulungu. Habakuku ananena kuti sanamvetse cifukwa comwe Mulungu anali kucitira izi. Anaona kuti lamulo inalibe mphamvu mu dziko.

Mu ndime 5 Mulungu auza Habakuku kuti anali pa nchito. Tanthauzo ndi lakuti iye anali kucitapo kanthu.

Habakuku 1:12-13 ionetsa kuti mayankho a Mulungu kwa Habakuku anamsokoneza. Mu ndime izi anafunsa mafunso ena. Coyamba, Habakuku anafunsa Mulungu ngati zinali

**MUTU 13
NCHITO YATHU YA CIYANJANITSO**

COLINGA: Ndidzaphunzira phunziro ili kundithandiza kudziwa kuti Mulungu andiyembekezera kutumikira ena.

MAU OYAMBA: Aroma 1:16, 15:7-33

NDIME ZA MPHUNZIRO YA LERO: Aroma 15:8-21.

MAU APAMTIMA: *“Koma zinthu zonse zicokera kwa Mulungu amene anatiyanjanitsa kwa iye yekha mwa Kristu, natipatsa utumiki wace wacyanjanitso.”* 2 Akolinto 5:18

Zaka zapitazo Mose anali kukhala mu mudzi wace. Tsiku lina kunalila lipenga lomwe anali kudziwa bwino. Onse anadziwa kuti cinthu coipa cadza pa mudzi, pena imfa.

Onse anadza pamodzi ndipo anamva kuti mwana wa mfumu wafa usiku. Anyamata anatumidwa kukanena za maliro kwa acibale.

Mose anapatsidwa njinga cifukwa anatumidwa ku mudzi wa kutali. Pa njira njinga inatha mphweya. Conco iye anapompa njinga ija. Koma njinga siinakhute, inali itabooka.

Akristu ena ali monga njinga yomwe yaphulika. Iwo sakhalanso anchito ai. Akristu otere sapereka uthenga wa Mulungu ku dziko. Mphamvu ya Mulungu ndi uthenga, mphamvu ya Mulungu ikhoza kuthandiza ife kukula monga Yesu. Akristu amagwira nchito pamene alola mphamvu ya Mulungu kukhala mwa iwo.

Kodi tikhoza kuthandiza bwanji mphamvu ya Mulungu mu dziko?

Paulo analemba kwa Akristu aku Roma kumuthandiza kumva colinga cace. Paulo ananena kuti uthenga upatsa mphamvu. *“Uthenga wabwino ukhoza kusintha anthu. Aliyense wokhulupirira mu uthenga adzalandira mphamvu ya Mulungu. Mphamvu ya Mulungu idzawathandiza kukula. Tsopano werengani mau a lero. Kodi Paulo anaonetsa citsanzo cabwino kwa Akristu?”*

sakanalowa mu bawa ngati akanadziwa kuti athu aja awiri anali kumuyangana. Palibe comwe cikanacitika kwa mbusa mu bawa, koma mamembala ace atsopano anakhumudwa.”

Pitilizani: “Nthawi zina ife timakhala monga Davide ndi Yohane. Tiona cinthu cina ciri kucitika ndipo timaweruza mwamsanga kopanda kudziwa bwino.

“Pali maphuziro awiri omwe tikhoza kuphunzira mu Aroma. Coyamba, Sitiyenera kuweruza ena. Caciwiri, sitiyenera kukhumudwitsa ena. Kodi muganizirapo nthawi ina pamene munaweruza munthu wina, kapena muganiza nthawi na pamene munaweruza wina ndi kuona kuti sicina coona. Kodi mufuna kuti mutiuze za nthawi imeneyo?”

Lolani nthawi kuti alankhuzane, ndipo apempheni ngati angaganizire njira ina yomwe akhoza kuthandizira Akristu ofoka. Auzeni kuti acite cimene aganiza kuti acite sabata ino. Aliyense akhoza kuganiza zomwe adzacita.

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero, kupempha Mulungu kuwathandiza kuthandiza abale ao ofoka sabata lino.

zoonadi kuti zonse zinali m’manja ace. Ndiponso anakhulupirira kuti zonse zidzayenda bwino ku mtundu wa Yuda. Mulungu sakanalola anthu ace osankhidwa kusautsidwa kapena kusakwaniritsa lonjezo. Anacha Mulungu kuti anali mwala kuonetsa kuti anali msamilo nthawi zonse.

Mu ndime 13, Habakuku afunsa Mulungu kuti adzayangana bwanji pa mtundu monga uwu woipa. Anali kunena kuti ngakhale kuti Yuda anali woipa sakanalingana ndi mitundu ina.

Mu ndime 1-4 ya mutu 2 itiuza kuti Habakuku anaimilira nji mu “ulonda.” Ici citanthauza kuti anaimilira nji pa maziko olimba omwe anali kupambana umoyo. Kumeneko anali kuyangana kwa Mulungu ku yankho ndi momwe akanayankha Mulungu.

Pamene Mulungu anaona Habakuku mu “ulonda wace” anayamba kumulangiza. Yankho inali mu maso mphenya. Maso mphenya ndi kuona kapena kudziwa cinthu comwe maso athu a umunthu sakhoza kuona.

Maso-mphenya anali a mtundu wonse osati cabe aneneri. Mulungu anauza Habakuku kuti alembe maso-mphenya pa magome a miyala. Anafunika kulemba kuti aliyense wopita mnjira akakhoze kuwerenga.

Ndime 4 ndi yankho ya mafunso ace. Ndi kumasulira kwa zonse zomwe zinabvuta mneneri. Anthu a ku Baubulo adzafa, koma okhulupirika adzakhala cifukwa ca cikhulupiriro cao.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA:

Lembani mau omwe sanathe pa bolodi kapena pa pepala. “Pamene ndiri ndi mabvuto, ndi...” Pamene akulu akulu abwera ku kalasi, auzeni kuti atsilize mau awa. Ena adzafuna mphindi zing’ono kuti aganizirepo. Apatseni nthawi.

Pamene aliyense akhala ndi nthawi ya kutsiliza mau aja, bwezerani zinthu zina zomwe mwanena. (Osanena kuti akakhala ndi mabvuto amalankhula ndi mkazi wace.” Koma nenani, “Tanena kuti ngati tiri ndi bvuto timalankhula ndi

akazi athu, timalankhula ndi akulu a nchito athu, timalankhula ndi akulu aku dela lathu.”)

Ena akhoza kunena kuti amapemphera kwa Mulungu pamene ali ndi bvuto. Ngati ndi tero, nenani kuti ena aife timapemphera pamene tiri ndi bvuto. Ngati palibe amene achula za pemphero, nenani “Tonse tiri ndi zozithandiziramo pamene tiri ndi mabvuto, koma njira yabwino ndi kupyolera mu pemphero.”

Pitilizani: Phunziro lathu lero ndi la nthawi pamene mtundu wa Yuda unali mu mabvuto. Munthu m’modzi anafuna kutsiliza mabvuto. Munthu m’meneyu, Habakuku, anapereka mabvuto ace kwa Mulungu.

KUMASULIRA

Patsani mapensulo ndi mapepala kwa aliyense amene akhoza kuwerenga. Auzeni kuti mudzafunsa mafunso mozungulira. (Onani kuti ophunzira anu akhala mozungulira.) Wophunzira aliyense atengeko ndime, ndipo alembe funso kucokera ku ndime.

Patsani ophunzira anu mphindi zing’ono kucita ici. (Wophunzira woyamba adzalemba funso kucokera ku Habakuku 1:2, wina Habakuku 1:3, conco basi)

Pamene atsiliza nchito yao, pemphani wina kuwerenga ndime zonse. Ndipo uzani wophunzira woyamba kufunsa funso lomwe alemba kwa wophunzira wa ciwiri. Onani kuti ayankha bwino. Wophunzira wa ciwiri afunsa wophunzira wa citatu ndipo acite tero mozungulira.

Pamene kalasi latsiliza mafunso onse, ayenera kuphunzira zambiri tsopano. Nenani, “Yuda anali mu msokonezo cifukwa ca macimo a mafumu. Mtundu unali utazadzidwa ndi cimo. Habakuku anafunsa Mulungu cimene analolera cithu cotere kupitilira. Ndipo Mulungu ananena kuti anali ndi njira ina. Njira imeneyi inali yakuti Babulo adzagonjetsa Yuda. Ici cinasokoneza Habakuku. Anafunsa Mulungu comwe analolera mtundu woipa kugonjetsa anthu osankhidwa. Mulungu anamuza kuti ao amene ali ndi miyoyo yoyera mokhulupirika, adzapulumutsidwa ndiponso ao amene ali oipa adzafa kuuzimu.

Nenani: “Davide ndi Yohane anaweruza mbusa wao pamene anaona iye ali kulowa mu bawa. Phunziro lathu lero ndi la ciweruzo monga cimenezi.”

KUMASULIRA

Kalasi litsegule mabuku ao ku Aroma 14:10-12, ndipo awerenge ndime zimenezo. Nenani: “Paulo anali kulankhula kwa abale ofoka ku mpingo wa ku Aroma. Anali kuwauza kuti asaweruze abale ao olimba. Mu mipingo yoyamba, kunali zobvuta zambiri pa kakhalidwe kabwino ka Akristu. Ambiri anazindikira ufulu omwe anali nao mwa Kristu. Awa anali Akristu olimba. Ena analandira Kristu ndi kuonjezera zinthu za tsopano zomwe anaganizira kuti Mkristu ayenera kukhala nazo kuonjezera ku malamulo akale omwe anali nao. Awa anali Akristu ofoka.” Pitilizani: “Nyama yonse pa nthawi imeneyi inali kuperekedwa ku mafano, ndipo inali kubweretse kwa ku mtsika kukaguli tsidwa. Malamulo akale ndi malamulo omwe Asaduke anaonjezera analetsa kudya nyama zina, makamaka yomwe inaperekedwa ku mafano monga nsembe. Akristu atsopano anakhulupirira kuti sanafunike kudya nyama ili yonse. Pamene anaona Akristu ena ali kudya nyama, anawaweruza, ndi kunena kuti sanali Akristu.”

Pemphani wina kuwerenga Aroma 14:13-23. Nenani: “Ndime izi zinali kwa Akristu olimba. Paulo anawauza kuti asaweruze abale ao ofoka. Ndiponso sanafunike kukhala okhumudwitsa anza. Anapitiliza kuwauza kuti cakudya sicalinali cinthu cofunikira kwambiri kuti cingakhudwitse wina kugwa. Pamene ciri conse comwe Mulungu analenga ciri cabwino kudya, Mkristu sayenera kupitiliza ufulu wace ndi kukhumudwitsa ena pakudya cinthu comwe wina aona kuti siciri cabwino kudya.”

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Nenani: Tiyeni tiganize za nthano la mbusa Emmanueli ndi mamembala ace awiri atsopano. Mbusa anali atalowa mu bawa kukatenga cinthu comwe wina anasiya. Anthu aja awiri sanaganize cinthu cabwino cimene mbusa akanalowera mu bawa. M’malo mwace anawaweruza iye ndipo cikhulupiriro cao cinacepera.” Pitilizani: “Mbusa analowa mu bawa osaona anthu aja awiri. Ngati iye akanawaona akanapita kwa iwo ndi kuwauza poyamba asanalowe mu bawa. Iye

Iye anatanthauza kuti tisalole cinthu cacing'ono monga kudya nyama kubweretsa mabvuto kwa munthu wina yemwe ali wofoka.

Ndime la 16 ndi lobvuta, koma litanthauza kuti cinthu cimene muyenera kucita siciyenera kukhumudwitsa anthu.

“Ufumu wa Mulungu” mu ndime la 17, itanthauza ulamuliro wa Mulungu womwe udzacitika mtsogolo.

Ndime la 23 iuza mbale wofoka kuti ngati samvera bwino pamene acita cinthu, ndiye kuti sayenera kucita cinthu cija. Cinthu ici ciri kwa Akristu onse. Ngati kudya kapena kumwa kutipangitsa ife kusamvera bwino, ndiye kuti tiyenera kusiya kucita zinthu zimenezo.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Nenani nthano ili: “Tsiku lina abwenzi awiri, Davide ndi Yohane, anali mu mtsika. Onse awiri anali Akristu atsopano, ndipo anali kulankhula za ulaliki omwe abusa anali atalalikira pa sabata.

“Davide anati, ‘Ndiwakonda abusa athu iwo amadziwa kulalikila bwino.’

“Yohane anabvomekezana naye, ndipo anati, ‘ndikhumbira kuti ndikadakhala monga iwo. Iwo adziwa zambiri za Mulungu.’

Koma pa nthawi imeneyo, Davide anayang'ana mu mseu ndipo anaona abusa ali kulowa mu bawa. Davide anadabwa ndipo sanakhoze kunena kanthu kali konse. Yohane anadabwa comwe cinacitika kwa iye. Ndipo Davide anati, ‘Yohane, abusa angolowa mu bawa posacedwapa.’

“Yohane sakhoze kukhulupirira zomwe bwenzi lace ananena. Onse anaima ndi kuganizira cocita. Yohane anati, ‘pena abusa athu si ali abwino monga momwe tinali kuganizira.’

“Pena ndi zoonza, anabvomekeza Davide. Anapita onse awiri ali ododoma mu mtima mwao. Palibe pa iwo awiri yemwe anadziwa kuti abusa analowa mu bawa muja kukatenga mapepala omwe anasiyidwa ndi mfumu.”

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani: Habakuku anadziwa kopita pamene anali ndi mabvuto. Anapita kwa Mulungu. Iye anayangana kwa Mulungu pa mabvuto ace onse. Mulungu anali wokhulupirika kwa Habakuku ndipo anayankha mafunso ace onse. Pa ndime ya 1 ndi pomwe Habakuku anapita pa nsanja ya olonda kukayembekezera yankho ya Mulungu. Tonse tiyenera kupeza malo omwe tikhoza kuthawirako pamene tipeza mabvuto. Itanthauza kuti Habakuku anazinyamula iye yekha kwa Mulungu. Sabata lino pamene tikhala ndi bvuto tiyetse kucita bwino. Nthawi zonse pamene tipeza bvuto tipemphere. Tipemphere kwa Mulungu pa zobvuta zathu, ndipo tiyembekezere yankho lace.

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero.

MUTU 2
KUKOMANA NDI KUSINTHIDWA

COLINGA: Phunziro ili idzandithandiza kumvetsetsa kuti cikhulupiriro mwa Mulungu cidzandithandiza kukomana ndi kasinthidwe komwe kamabwera nthawi zonse mu umoyo wanga.

MAU OYAMBA: Salmo 137:1-6, Yeremiya 29

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Yeremiya 29:1-11

MAU APAMTIMA: *“Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingilira inu, ati Yehova, malingiliro a mtendere, si a coipa akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezo.”* Yeremiya 29:11

Agogo anga anafa kale-kale. Iwo sanaonepo njinga. Sanaonepo wailesi kapena kuganizira kuti munthu akanakhoza kuyenda ku mwezi.

Zinthu zambiri zimasintha. Caka ciri conse cimakhala cobvuta kwa ife kutsatira kasinthidwe kameneka. Kasinthidwe kena ka mabweretsa mantha. Umoyo suoneka bwino pamene kasinthidwe kabwera msanga. sitikhoza kuletsa zinthu kuti zisasinthe koma kodi tikhoza kuphunzira kutsatira kasinthidwe? Anthu a Mulungu anakomana ndi zinthu zambiri zosintha pamene anatengedwa ku Babuloni. Kodi iwo anakwanitsa bwanji? Werengani Yeremiya 29:1, 4-11, kukuthandizani kuyankha funso.

DZIKO LA CILENDO

Nthawi inafika pamene mfumu ina yochedwa Yosiyā inayesa kubweretsa Ahebri kwa Mulungu. Yosiyā anali mfumu yabwino, koma anthu sanali okhulupirika kwa iye, maka-maka ku zinthu za umulungu. Cifukwa ca kusamvera kwao ndi kusakhulupirika, Mulungu analola kuti atengedwe.

Nthawi ya Yosiyā, Mulungu anaitana Yeremiya kukhala mneneri. Ananenera kuti Mulungu adzalola nkondo kudza kwa iwo. (Onani Yeremiya 4:19) koma anthu sanamvere. Mafumu omwe anabwera Yosiyā atafa naonso sanamvere. Ici cinakwiitsa Mulungu conco, pamene Yohaekimu anali mfumu ya Yuda, mfumu Nebukadinezara wa ku Babulo

MUTU 12
KWA MPHUNZITSI

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kuganizira njira imodzi yomwe iwo akhoza kuthandiziramo Akristu ofoka.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Palibe

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Mu Aroma 14: 10-23 Paulo anena kwa onse Akristu ofoka ndiponso olimba. Kwa iwo ali kuwauza kuti asiye kuweruzana wina ndi mnzace.

Mu Aroma 14:10-12, Paulo analankhula coyamba kwa Akristu ofoka mu mpingo. Iwo anali kubweretsa mtsokonezo mu mpingo za kakhaliidwe. Makhaliidwe ao sanali opambana abale ao olimba. Koma abale ao olimba naonso analibe khalidwe lopambana.

Cidzakhala cabwino kuwerenga 1 Akorinto 8-10 kuti mupeze zomwe Paulo analemba kwa Mpingo wa ku Akorinto. Kunali nkhani yaikulu yomwe inabwera cifukwa ca kudya nyama. Akristu olimba sanaone kulakwa pakudya nyama ya kumtsika. Indedi panalibe coipa pa kudya nyama. Koma panali tImagulu timene tinaika malamulo pakudya nyama. Kalata iyi kwa Aroma inalembedwa ku Akorinto. Kapena mu Aroma munalibe bvuto la kudya nyama. Koma Paulo anada nkhwana ndi nkhani yomwe inali mu Akorinto.

Mu ndime izi Paulo anali kungonena kuti asaweruze makhaliidwe a abale ao. Kuuza abale ao mayendedwe sikunali kulimbikitsa cikhulupiriro cao.

Mu Aroma 14:13-23 Paulo analankhula kwa abale olimba. Anawauza kuti sanafunike kuweruza abale ao. Ndipo sanafunike kukhala obweza anzaao kumbuyo. Ngati kudya nyama kunabwetsa mabvuto kwa Akristu ofoka, Akristu olimba sanafunike kudya nyama.

Paulo iye anazindikira kuti kudya nyama sikunali coipa. Ici cinatanthauza kuti Paulo anali mbali ya thupi limodzi la Kristu ndiponso wotsogoleleredwa ndi Mzimu Woyera.

Ayeneranso kumanga wina ndi mnzace mu cikhulupiiriro cao. Mkristu asadye kapena kumwa cinthu comwe r. bale wace adzakhumudwa naco.

Ngati muganiza kuti mudziwa zonse Mulungu afuna kuti mucite, nenani tero. Mkristu aliyense adzayankha kwa Mulungu zomwe acita. Palibe amene ayenera kukakamidza mzace zomwe ayenera kucita. Akristu ayenera kuyenda mu cikondi. Mu ndime 23 Paulo sanali kulankhula za cimo monga nsanje ndi dyela. Macimo otere onse ndi oipa. Ngati munthu aganiza kuti cimene acita coipa asacite. Iwo angapangitse Akristu ofoka kugwa. Kodi muli olola kuthandiza mbale wanu?

analowa mu Yerusalemu ndi kuwatenga kuukapolo. Anabwereranso ndi kutenga onse amene anali akaswili ogwira zi nchito zosiyana-siyana. Okhao amene sanali akaswili ndi amene anasala. Ayuda anali mu manja mwao. Iwo tsopano anali kukhala mu dziko lacilendo. Sanamvetse cifukwa comwe Mulungu analola dziko loipitsitsa kuwatenga kuukapolo. 'Iwo anasiya kacisi lao lomwe linafunika kupembezeramo. Iwo anasiyanso ena mwa mabanja ao mu Yuda. Iwo anaona Yerusalemu ili kuonongedwa. Pamene anali kutengedwa sanadziwe kuti idzabweranso.

“Ku mitsinje ya ku Babulo, kumeneko tinakhala pansu, inde tinalira, pokumbukira Ziyoni. Pa msondodzi uli m'mwemo tinapacika mazeze athu. Popeza pamenepo akutigwirawo anatifunsa nyimbo, ndipo akutizunza anafuna tisekere, ndi kuti, mutiyimbire nyimbo imodzi ya ku Ziyoni. Tidati, tidzayimba bwanji nyimbo ya Yehova m'dziko lacilendo? (Salmo 137:1-4)

“Kasinthidwe kotero kanali kakukulu.” Ayuda anaganiza tero. Ayuda sanafune kuyimba. Iwo anali kudziwa nyimbo za Ziyoni, koma iwo anafuna kulira pamene akuwazunza awauza kuyimba. Sanaone ciyembekezo mu umoyo wao ngakhale wa kutsogolo, popeza anali, m'manja mwa akuwazunza.

Analibe ufulu, anadziwanso kuti sakanakhoza kusintha kanthu kali konse. Onse anadziwa ici. Mfumu Nebukadinezara sakawalola kuwamasula. Kodi iwo acite ciani kuti asiye kulila?

KODI IWO AKANATENGA BWANJI KASINTHIDWE KOTERE?

Yeremiya, mneneri, sanapite nao ku Babulo. Iye anatsara mu Yerusalemu.

Anadziwa kuti anthu omwe anategedwa kuukapolo anali mu mabvuto. Mulungu anamuuzza kuti anthu sadzabwerera kwao mwamsanga. Conco Yeremiya analemba kalata kwa akapolo ku Babulo. Anawauza kuti Mulungu sanawaiwale.

KOMANANI NDI DZIKO LIRI KUSINTHA

Yeremiya anafunira mafuno abwino ao omwe anali muukapolo. Anafuna kuti iwo adziwe coonadi, kuti iwo

adzakhala mu Babulo dzaka zambiri. Iwo anafunika kubvomereza zonse monga momwe zinaliri. Iwo sanakhoze kubwerera ku Yerusalemu. Mulungu anafuna ayambenso umoyo watsopano.

Yeremiya anawauza kuti acite zinthu monga anali kucitira mu Yuda, dziko lao loona, "Mangani nyumba, kwatirani ndi kukhala ndi ana." Ici sicinali cisankho ca Yeremiya, koma ca Mulungu. Mulungu anawauza kucha Babulo dziko lao. Anafuna kuti akhale a mtendere mu Babulo. Njira yokha yomwe akanapedza mtendere ndi kupitira mu mapemphero. Pamenepo aneneri abodza anapedza mpata onena za bodza. Analalikira kuti ufulu unali pafupi. Iyi inali bodza ku zomwe Mulungu ananena.

Pa kunena ici anafuna kuti anthu aukire mfumu Nebukadnezara. Mulungu anawauza kuti asakhulupirire mu aneneri abodza. Mulungu anawalonjeza zinthu zabwino. Tsiku lina miyoyo yao idzasintha.

Pamene iwo anali kuyembekeza, Mulungu anali nao. Mulungu anali mu Babulo ndi mu Yuda. Anawadalitsa pamene iwo anali mu masinthidwe mu dziko la cilendo. Iwo sanafunike kutaya cikhulupiriro. Analota kubwerera kwao. Tsiku lina loto lao likakhala loona. Mulungu anadziwa malingaliro omwe anali nao pa iwo. Malingaliro ace anali abwino. Anawapatsa ciyembekezo.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi kasinthidwe ka umoyo kakuza inu? kodi cikhulupiriro mwa mphamvu ya Mulungu cikupatsani ciyembekedzo ndi kukuthandizani kukomana ndi kasinthidwe? Kodi mudzamvera Mau a Mulungu ndi kusasocetsedwa ndi atsogoleri abodza? Kodi muli ndi ciyembekedzo, kuti Mulungu acite cifuniro cace mu dziko?

Pemphererani thandizo la Mulungu mu nkhani izi.

anali omasuka mwa Yesu. Iwo anadya nyama ili yonse yabwino kudyedwa. Ofoka mu cikhulupiriro anagwirirabe kuzikhulupirira zakale. Iwo anakhulupirira kuti anacimwa ngati adya nyama yomwe inaperekedwe monga nsembe. Anatero, cifukwa anali ofoka mucikhulupiriro cao. Paulo anauza Akristu a ku Roma kuti asapeze cifukwa kwa wina ndi mzace. Mulungu sanawapange kuti akhale oweruzana. "...comwe Mulungu wayeretsa, usache codetsedwa" (Macitidwe 10:15).

USAKHUMUDWITSE MBALE WAKO

Werengani ndime 14-18. Anthu ambiri masiku ano adziwa za mpira. Kumakhala woyang'anira, ndi magulu awiri. Gulu lina likhoza kukhala litaphunzira kwambiri, koma gulu lina lofoka. Gulu lofoka silizaonetsa mphamvu ngati gulu lija lamphamvu liri kuonetsa mphamvu zace poyamba. Gulu lolimba likhoza kulimbikitsa lina mu cianjano cao. Koma ngati iwo sanacite bwino amaononga cilimbitso ca gulu lija.

Ziyenera kukhala tere ndi Akristu. Akristu olimba ayenera kusamala zomwe acita. Ngati kacitidwe kanu kapangitsa wina kugwa, ndiye kuti musacite cinthu cija. Onetsani Akristu ofoka momwe Akristu akhalira mu umoyo wa Cikristu. Aphunzitseni kumanga cikhulupiriro cao mwa Kristu. Athandizeni kukula kuuzimu.

Pamene munthu akhala Mkristu, sindiye kuti ndi wokhwima. Ayenera kukula. Akali mwana muuzimu. Tonse tidziwa kuti mwana afunika kusamalidwa. Paulo anena kuti Akristu olimba sayenera kupangitsa abale ao kugwa kuuzimu. Monga Akristu sitiyenera kucita cinthu comwe sicili cabwino kwa abale athu. Comwe tikhoza kucita cikhoza kukhala coipa kwa ena.

Akristu ayenera kuthandiza ena kupeza mtendere ndi cikondwerero. Ici cidzakondweretsa Mulungu. Ufumu wace udzadza ngati titero. Ufumu wa Mulungu uli kale pano ndi umoyo wabwino, mtendere, cikondwerero zomwe zipatsidwa ndi Mzimu Woyera kwa okhulupirira mwa Yesu.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Paulo anauza Akristu aku Roma momwe akanakhalira umoyo wa Cikristu. Werengani ndime 19:23. Akristu ayenera, kucita zinthu zomwe zibweretsa mtendere.

MUTU 12
KUYENDA MU CIKONDI

COLINGA: Phunziro idzandithandiza, kuthandiza Akristu ofoka.

MAU OYAMBA: Aroma 14:1-15:6; 1 Akorinto 8

NDIME ZA MPHUNZIRO YA LERO: Aroma 14:10-23

MAU APAMTIMA: “Cifukwa cace tisaweruzane wina ndi mnzace; koma weruzani ici makamaka, kuti munthu asaike cokhumudwitsa pa njira ya mbale wace kapena comphunthwitsa.” Aroma 14:13

Akristu ena ndi olimba mu zikhulupiriro zao. Ena ndi ofoka muzikhulupiriro zao. Mnyamata wochedwa John anapita kusukulu la kutali caka coyamba. Maonekedwe ace anali wa mng’ono. Anzace ena anamseka cifukwa ca maonekedwe ace. John anali Mkristu. Akristu ena anayamba kumuthandiza. Iye sanadziwe cilankhulidwe cacizungu, koma anayetsetsa. Akristu anali acifundo kwa iye. Anamulimbikitsa. Cinapangitsa John kukhala Mkristu wolimba.

AKRISTU A CIROMA

Werengani Aroma 14:10-23. Akristu ena mu Roma anali Akristu ofoka. Ena anali olimba. Mamembala ena a Ciyuda anali anafokera. Iwo anaphunzitsidwa kuti asadye zakudya zina. Tsopano anali Akristu. Kodi akanatani? Iwo anaganiza kuti idzakhala cimo kudya nyama yomwe analetsedwa. Iwo anafuna kuti akhale bwino mu mtima mwao ndi mukacitidwe ka cipembedzo.

Kudya nyama sikupulumutsa munthu. Ndiponso kudya nyama sikupangitsa munthu kucimwa. Koma ngati wina aganiza kuti ngoipa kuteri, koma apitiliza ndi kudya, imakhala cimo. Kodi Paulo anauza ciani Akristu a ku Roma za izi?

MUSAWERUZE MBALE WAKO


Mpingo wa ku Roma unali ndi magulu awiri. Paulo anachagula loyamba lolimba mu cikhulupiriro ndi lina lofoka mu cikhulupiriro cao. Olimba mwa Ambuye anakhulupirira kuti

MUTU 2
KWA MPHUNZITSI


COLINGA: Umoyo umasintha nthawi zonse. Ndifuna ophunzira anga kukhala ndi cikhulupiriro mwa Mulungu kuti pamene akhala adziwe kuti zonse ziri m’manja a Mulungu.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Lero mudzayamba mndandanda wa nthawi. Kwa ici mudzafunika pepala lalikulu. Tengani mapepala ndi kuwaika pamodzi ndi (glue) kapena comatira kapena maphini. Ikani pepala ili pa cipupa pomwe ophunzira akhoza kuliona nthawi iliyonse pamene abwera mu kalasi.

Lembani mdzere pakati pa pepala. Uwu ndi mdzere wa nthawi. Lembani mdzere uwu ndipo pansu pace lembani: “Habakuku adandaula kwa Mulungu.” Mdzere wanu udzaoneka tere:



Mu nthawi ya phunziro, mudzaonjezera cinthu cina, kuti pakutha kwa mdzere wa nthawi udzaoneka monga tere:



Onani kuti mdzere wanu uoneka monga mdzere woyamba. Pamene muli kuphunzitsa mudzaonjezera cinthu cina comwe cinacitika. Sungani mdzere kuti mukagwiritse nchito sabata lotsatira. Pamene mutsiliza pa masabata atatu mudzakhala ndi zinthu zinai zolembapo. Mukhalenso ndi mapepala ndi mapensulo.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA:

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Zinthu zomwe zicitika mu phunziro zicokera mu Yeremiya 29:1-11. Zinacitika patapita zaka 9 kapena 10 Habakuku atapita pa nsanja ya ulonda. (Kucokera ku phunziro latha.) Anthu a ku Babulo anali atagonjetsa Yerusalemu ndi kutenga anthu acifumu ndi ena ophunzira. Akapolo amenewa anatengedwa ku Babulo.

Pamene anthu amenewa atakhala ku ukapolo kwa zaka zing'ono anapatsidwa ufulu mu mzinda. Pa anthu amenewa panali aneneri oipa. Aneneri amenewa anali kuuza anthu kuti adzabwerera posacedwa. Cinenero caboza ici cinali kusokoneza anthu. Yeremiya anawalembera kuwauza kuti akonzekere kukomana ndi kasinthidwe komwe anakomana nako mu umoyo wao.

Mu ndime 1-3 inena za kalata yomwe inatumizidwa ku Babuloni. Elasa pena anali mbale wace wa Ahikamu yemwe anaimilira Yeremiya pamene anagwiridwa. (Mu phunziro loyamba). Gamariya anali ndi danga la kumvera baruki ali kuwerenga mphukutu mu m'nyumba yace. (Onani mutu 36:10) Anthu amenewa pena anatumizidwa kwa Nebukadnezara kucokera kwa mfumu Zedekiya kupereka misonkho. Yeremiya anatumiza kalata wace. Ndime 4-7 iyamba ndi kalata. Ayamba ndi mau awa. "Ambuye wa makamu akuti," ndiye momwe manenero anali kuyambira.

Ambuye anauza anthu a Ciyuda kuti akhale ku Babuloni. Iwo sanabwerere kwao kufikira zaka 70 zitapita. 70 ndi nambara mu Cipanagano Cakale yomwe inatanthauza la ngwiro.

Ndime 5-9 ndi cenjenjezo la kwa aneneri aboza omwe anali ku Babulo.

Ndime 10-11 ipatsa citsimikizo kwa ambuye kuti anthu onse anali akali anthu ace osankhidwa. Iye sanaiwale ndipo anali akali kupanga njira.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO:

KUDZIWITSA:

Nenani: Mu mutu woyamba tinanena zomwe zimacitika pamene timalowa mu mabvuto. Pamene tilankhula za

womwe upezeka pa zothandizira pa kuphunzitsa, werengani mphatso za Mzimu Woyera. Cifukwa cinenero cinena kuti ndi kulalikira kapena kugawa uthenga wa Yesu. "Mzimu wa cinenero" ndi kukhala ndi luso la kuzindikira mizimu. Mphatso ina ndi ya kulimbikitsa. Mphatso kusamalira ena. Ina ndi ya kukhala ndi luso la kudziwa zinthu. Mphatso ina ndi ya kukhala ndi luso la kutsogolera gulu la anthu. Iyi iyenera kukhala nthawi ya kudziwa zinthu zambiri kwa kalasi lanu. Ena adzakana kuti alibe mphatso zomwe ena akhoza kuchula mwa iwo, koma alimbikitseni kuti anthu amazindikira za mphatso zathu pamene ife eni ace tisanadziwe.

Tsekani mtsonkhano ndi pemhpero ya ciyamiko cifukwa ca mphatso zomwe Mulungu apatsa yense wa ife.

KUMASULIRA

Ophunzira anu atsegule mabuku ao ku Aroma 12. Wina awerenge ndime zoyamba ziwiri. Nenani: "Mutu uwu unalembedwa kwa munthu aliyense payekha ndiponso kwa Mpingo. Ndime ziwiri zoyamba ndi za kwa munthu pa yekha. Kodi ndime izi zitiuza ciani? (Kupereka matupi athu monga nsembe zamoyo)"

Funsani: "Kodi tingapereke matupi athu bwanji monga nsembe zamoyo? Patsani nthawi kuti alankhuzane, ndipo tsogolerani kalasi kunena zomwe Paulo ananena kuti ayenera kupereka miyoyo yao ku nchito yace"

Funsani: "Kodi citanthauza ciani kukhala monga munthu aliyense mu dziko?"

Funsani: "Kodi tingasinthidwe bwanji? (Pa kuwerenga Buku Lopatulika, ndi kulankhula ndi Akristu ena.)"

Wina awerenge ndime 3-8. Nenani: "Patapita nthawi mu phunziro ili tidzatenga nthawi pa kuyang'ana pa mphatso za kuuzimu zomwe Mulungu atipatsa. Tsopano lino tiyeni tione kuti Paulo ananena kuti tiyenera kugwiritsa nchito izi kumangilira thupi la Kristu."

Werengani Aroma 12:9-21. Nenani: Ndime izi zitiuza kuti tiyenera kukhala monga Akristu. Nenani khalidwe limodzi la Akristu." Aloleni kuti anene makhalidwe onse amene anenedwa mu ndime izi. (Kukhala acikondi, opatsa, olila ndi amene alila, kubwezera cabwino ku coipa ndi zina) Onani kuti anena zonse zomwe zapatsidwa apa.

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Nenani: Yense wa ife ali ndi mphatso za Mzimu. Ndidzawerenga mndandanda wa mphatso zimenezi zomwe Mzimu Woyera upatsa. Uwu simundandanda wonse. Iwo uikaponso mndandanda womwe upezeka mu Aroma, 1 Akorinto ndi Aefeso. Ndizamasulira cifukwa cotipatsira mphatso zina. Pamene nditsiliza kuwerenga mndandanda tidzawerenganso, ndipo ndifuna kuti aliyense wa ife aganize munthu yemwe ali ndi mphatso zimenezi. Pamene ndidzabwezeranso kuwerenga mndandanda, ndifuna inu kuchula dzina la munthu yemwe muganiza kuti ali ndi mphatso imeneyi. "Tsopano kugwirisa nchito mndandanda

mabvuto, timapeza thandizo. Tiyenera kupemphera pa bvuto ili lonse. Phunziro lathu lero litiphunzitsa kuti Mulungu amaika anzeru pa anthu ace.

"Mau athu apa mtima a lero ndi ndime ya cilimbitso. Ndifuna kuti tilembe pansu. Idzakutsimikizani inu."

Patsani mapensulo ndi mapepala kwa aliyense. Mulembe ndime pa bolodi kapena pa pepala lalikulu, ndipo iwo adzalemba zomwe inu mwalembe. Ngati anthu anu sakhoza kuwerenga ena akhoza kuwalembera.

KUMASULIRA

Ophunzira anu atsegule mu mabuku Opatulika ao. Pemphani wina kuwerenga Yeremiya 29:1-3. Nenani, "Sabata latha tinaphunzira za Habakuku, analankhula ndi Mulungu za zinthu zomwe zinali kucitika kwa Yuda. Kodi Mulungu anamuuzza ciani? (Mulungu anamuuzza kuti anthu a ku Babulo adzagonjetsa Yuda)"

Nenani, yang'anani pa mdzere wa nthawi yomwe mwalembe. Tiona kuti Habakuku anadandaula kwa Mulungu pa nthawi ya 605 b.c. B.c. itanthauza pamene Yesu asanabadwe. Ndipo zaka zinalembedwa kucokera ku mbuyo. Atha kulankhula ndi Habakuku, Babulo linabwera ndi kugonjetsa Yerusalemu. Anthu ambiri odziwika mu Yerusalemu anatengedwa ku Babuloni." Ayuda anali atakhala zaka zing'ono mu Babulo pamene Yeremiya analemba kalata yomwe ndime ili kunena. Iwo sanali okondwa kumeneko. Anafuna kubwerera kwao. Pakati pa iwo panali aneneri aboza omwe anali kunena kuti adzabwezera posacedwa. Ici si cinali colinga ca Mulungu conco anauza Yeremiya kuwalembera. Tiyeni tiwerenge ndime 4-7 ndi kuona zomwe Mulungu analangiza ayuda kucita.

Ndime ziwerengedwe nenani," Manenero onse anali kuyamba ndi mau akuti "Ambuye akuti." Ici cinaonetsa Ayuda kuti mau anali a Mulungu. Kodi Mulungu anauza ciani anthu? (Lolani kalasi lanu ilankhuzane.) Tsilizani pakunena zomwe Habakuku ananena pa kuyembekeza kasinthidwe mu umoyo wao.

Funsani, “Ncifukwa nciani anawauza kupempherera Babulo? (Kuonetsa kuti adzamva ndi kuyankha mapemphero ao ngakhale sanapemphereredwe mu Yerusalemu.

Werengani ndime 5 ndi 9. Nenani, “Ndipo Mulungu anapatsa Ayuda mau acitonthozo apa. Iye adzabwezera Ayuda ku Yerusalemu. Anali ndi colinga cao. Cinali cowatsimikiza.”

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani, “Tsopano tidzaonjezera ku mdzere wa nthawi yathu. Onjezerani zaka ndi zinthu zina monga momwe muonera mu zothandinzira pa kuphunzitsa. Nenani: Mudzaona kuti zaka zicepela pamene nthawi ili kupitilira. Tidzaonjezera zinthu zina zocitika mu mzere wathu kumasabata awiri otsatira.

“Mulungu akali ndi colinga ca ana ace. Pamene tikoma ndi kasinthidwe, nthawi zina tikhoza kuganiza kuti Mulungu satifuna koma, sitero ai. Atikonda ife ndipo amakhalapo pamene kasinthidwe kabwera mu umoyo wathu. Cinthu cina cacikulu ndi kasinthidwe ka matupi athu. Kasinthidwe kena ndi kacitukuko mu dziko lathu. Mulungu atikonda ife mukasinthidwe kalikonse. Kodi ndi kasinthidwe kotani kamene munakomana nako? Kodi munapambana? Patsani ophunzira nthawi kulankhuzana mafunso. Ndipo pempherani kuti Mulungu apitilize kuthandiza kalasi lanu kukhala Akristu olimba mu nthawi ya kasinthidwe.

Mipingo yathu ifunika kuona mphatso za kuuzimu mwa mamembala ace ndi kuwalola kucita nchito.

Aroma 12:9-21 iuza aliyense ndiponso monga mpingo momwe angakhali wina ndi mzace.

Coyamba, tiyenera kukondana zoon. Ici ndi cobvuta masiku ano mu mipingo yathu. Anthu sadziwana bwino-bwino. Kodi angakondane bwani?.

Tiyenera kuda comwe ciri coipa. Cinanenedwa kuti anthu amaopa zotsatira zace za cimo koma saopa cimo. Ngati cimo imatipangitsa kumva kuipa ndiye kuti tiyenera kuda cimo.

Tiyenera kupatsa wina ndi mnzace ulemu. Ici citanthauza kuika mnzako pa tsogolo pa ife, kumuika mu malo oyamba. Tiyenera nthawi zonse kukhala otumikira, Akristu ayenera kukhala okhulupirika nthawi zonse kucita nchito ya Mulungu malinga Mulungu awapatsa mphamvu.

Tiyenera kukhala omasuka pa kupereka kwathu ndiponso kutsegula nyumba zathu kwa ena. Tiyenera kukondwera ndi omwe ali kukondwera. Nthawi zambiri timacita nsanje ndi anzathu omwe ali kukondwera ndipo sitimakondwera nao. Uku ndi kulakwa tiyenera kulila ndi iwo amene alila. Icinso ndi cobvuta kucita.

Tiyenera kusiya kuti Mulungu ndiye amene adzabwezera coipa. Ngati wina aticitira coipa ife tiyenera, kumucitira zabwino ndi kusiya zonse kwa Mulungu.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO ILI

KUDZIWITSA

Funsani: “Kodi mudziwa munthu wina mu mpingo wanu yemwe ali ndi mphatso ina ya padela?”

Ngati kalasi lanu lakhala liri kukomana kwa nthawi yaitali, iwo adzakhoza kunena mphatso zina zomwe anthu ali nazo, ngakhale za aphunzitsi omwe. Ngati kalasi lanu ndi latsopano kapeña muli Akristu atsopano, iwo sadzakhoza kuyankha mafunso.

Mutatha kulankhuzana, nenani: “Mulungu kupyolera mwa Mzimu Woyera apatsa aliyense mphatso za Mzimu Woyera. Ili ndilo phunziro lathu la lero.”

MUTU 11
KWA MPHUNZITSI

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kuyamba kuona mphatso zao zomwe Mulungu anawapatsa kuzigwiritsa mu mpingo.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Mudzafunika mndandanda wa mphatso za kuuzimu: Cinenero, mzimu wa cinenero, ubusa, cikhulupiriro, Kufalitsa, utumwi, zodabwitsa, kuthandiza, cifundo, kupatsa, kuciritsa, nzeru, ciphunzitsa, ndi utsogoleri.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Aroma 12 apatsa malangizo kwa munthu aliyense ndiponso kwa mpingo. Aroma 12:1-2 ndi ndime zomwe zimanenendwa kwambiri. Paulo anakakamiza Akristu kupereka matupi ao monga nsembe za moyo kwa Mulungu. Nsembe ya moyo inena kuti matupi athu ayenera kukhala monga mwini wace. Anthu ambiri aganiza kuti nthawi ya kupembedza ndi nthawi yomwe timapita ku mpingo kukapemphera, kuyimba ndi kumva ulaliki. Paulo alikunena kuti tiyenera kupereka umoyo wathu wamasiku onse kwa Mulungu kucipembedzo. Kodi tingacite motani? Ticita pa 'rugawana mu Cikristu, pa kuonetsa cikoŋdi kwa ena.

Paulo anena kuti sitifunika kutenga maonekedwe a dziko lino. M'malo ace tifunika kusinthidwa. Ici cicitika kupyolera mu kuyenda ndi Mulungu, kupemphera, kuwerenga Buku Lopatulika, kulankhuzana ndi abwenzi a Cikristu ndi kukhulupirira Mulungu.

Aroma 12:3-8 ilankhula ku mpingo. Tonse tiri mbali ya thupi limodzi. Mu thupi la munthu, dzanja silikhala lokwiya ndi khosi. Mwendo sunena kuti iwo uli wopambana anzace. Thupi lonse ligwira nchito pamodzi kucitira zabwino. Mkristu aliyense anapatsidwa mphatso la Mzimu Woyera. Ena anapatsidwa mphatso zambiri. Mphatso zonse ziyenera kugwira nchito kucitira ubwino mpingo. Ndico cifukwa cace mphatso zinapatsidwa. Mulungu apatsa matupi okwanira.

MUTU 3
KUSUNGA CIKHULUPIRIRO

COLINGA: Ndidzaphunzira kuti ndifunika kusunga cikhulupiriro molimba ndiponso coona.

MAU OYAMBA: Danieli 1, 6

NDIME ZAMPHUNZIRO LA LERO: Danieli 1:3-5, 1-10, 18-19, 6:10, 21-22.

MAU APAMTIMA: "...*Alemekezedwe Mulungu wa Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, amene anatuma uthenga wace napulumutsa atumiki ace omkhulupirira iye, nasanduliza mau a ine mfumu, napereka matupi ao kuti asatumikire kapena kulambira Mulungu wina yense koma Mulungu wao wao.*" Danieli 3:28

Zaka zapitazo, Yohane pamodzi ndi banja lace anapita ku dziko lacilendo. Iwo anapeza mipingo ing'ono ya Baptist. Koma ici sicinawalepheretse kupita kumpingo. Anasunga cikhulupiriro cao ndipo posacedwa anayamba mpingo watsopano.

Nebukadinezara anagonjetsa a Yuda. Iye anatenga Ahebri omwe anali amphamvu ku Babulo. Anakhala ku dziko lacilendo. Yeremiya, mneneri anawauza kupanga Babulo kukhala monga kwao. Kodi iwo akanakhoza kusunga cikhulupiriro cao?

ACINYAMATA ACIHEBRI ASANKHIDWA

Werengani Danieli 1:3-5, 9-10, 18-19, 6:10, 21-22. Mfumu Nebukadinezara anafuna anyamata aci Hebri kuphunzitsidwa kuti akatumikire mu nyumba yace. "Ndifuna anyamata aci Hebri. Ayenera kukhala olimba, anthanzi, ophunzira, audongo, omwe aphunzira msanga, ndiponso a maonekedwe abwino." Mfumu inatero kwa kapita wa Ashipenazi.

Anyamata amenewa anafunika kuphunzitsidwa. Kwa zaka zitatu anafunika kuphunzira kulemba ndi kuwerenga. Anawa anapatsidwa danga la kukhala ndi kudza mu nyumba ya Mfumu. Mfumu Nebukadinezera anafunika kuwayesa,

ndi kusankha omwe anaoneka bwino kutumikira mu nyumba yace.

Danieli pamodzi ndi abwenzi ace anasankhidwa kuti akaphunzire. Anafunika kupatsidwa maina atsopano. (Onani ndime 6:7) Danieli anachedwa Beltishazar, Shadreki anachedwa Hananiya, Meshaki anachedwa Mishaeli ndipo Abedenigo anachedwa Azariya.

PEMPHO LA DANIELI

Cifukwa ca lamulo lapadera pa zakudya, Danieli anaganiza kuti iye pamodzi ndi abwenzi ace asadye cakudya ndi vinyo. (Werengani ndime 8) Danieli anapempha wa nchito kuwalola kudya ndiwo za masamba ndi madzi cabe. Iwo anafuna kusunga malamulo a Mulungu. Iyi ndiyo inali yesero yoyamba ya Danieli. “Ndicofunikira kumvera Mulungu kupambana mfumu.”

Iyi inali yesero loyamba la cikhulupiriro ca Danieli. Iye akanataya mwai wace wakukonedwa ndi mfumu. “Ciri cofunikira kumvera Mulungu kopambana mfumu,” Danieli anaganiza tero.

Mu ndime 9-10. Tiona kuti wa nchito uja anakonda Danieli. Anali okonzekera kulandira pempho la Danieli, koma anali ndi mantha. Iye anaganiza kuti Danieli pamodzi ndi abwenzi ace sadzaoneka bwino. Mulungu anaika mtima wabwino mwa wa nchito uja. Koma anaopa kuti pena anyamata aja sadzaoneka bwino.

Danieli anauza wa nchito uja kuwapatsa ndiwo za masamba kwa masiku khumi, kuti aone ngati adzaoneka bwino. Ngati sitero, akanadya cakudya ca mfumu. Patapita masiku khumi Danieli pamodzi ndi abwenzi ace anaoneka anthanzi kwambiri kupambana ena. Conco anawalola kupitiliza kudya ndiwo za masamba ndi madzi.

AMUNA ANAI ASANKHIDWA

Anyamata amenewa anapitiridza kudya cakudya cimenezi kwa zaka zitatu. Iwo anakhala olimba, ndipo anaphunzira zonse zomwe anaphunzitsidwa.

Danieli ndi abwenzi ace anasankhidwa. Iwo anaoneka anthanzi kupambana ena ndipo anzeru zakuya. Mulungu

4. Kulimbikitsa (Ndime 8) ulaliki wa Mulungu kulimbikira ena. Afunika kulimbikitsa kutumikira ndi mtima wonse.

5. Kuthandiza - kugawana (ndime 8) ithandiza Akristu kugawana zomwe ali nazo ndi ena. Agawa ndalama, cikondi ndi cifundo cace.

CIKONDI MU UMOYO WA MASIKU ONSE

Werengani Aroma 12:9-21. Ndime 9-13 itiuza momwe Akristu ayenera kukhalira funani-funani njira zomwe mukhoza kukhala umoyo wa cingonjetso. Akristu ayenera kudana ndi coipa ndi kugwirira ku coipa. Ayenera kukhala okhulupirika wina ndi mzace, mwa cikondi.

Tiri mu masiku a cikondi copanga pa kanema ndi pa wailesi. Koma tifunika cikondi coona pamene tikahal wina ndi mnzace. Tiyenera kuonetsa mzimu wakutumikira Ambuye ndi cikondwerero. Pamene Akristu ali ndi mabvuto, ayenera kupemphera, kukhala oleza mtima ndi kukondwera. Ici cikhoza kucitika cifukwa ca ciyembekezo mwa Yesu Kristu. Iwo ayenera kugawana zomwe ali nazo ndi ena. Akristu oyamba anakakamizidwa kulandira alendo mu nyumba zao. Inali danga la kucitira umboni ndi kugawana cikondi ca Yesu.

Akristu a ku Roma anakakamizidwa kukondana wina ndi mnzace. Akristu anabvutika mu malo ambiri monga momwe timabvutikira masiku ano. Paulo anati kwa iwo “Pemphererani akukubvutitsani kuti apulumutsidwe.” Pena ena iwo anapeza ici kukhala cobvutitsa. Koma Paulo analemba kucera ku Cipangano Cakale ndime ya 20 kuwaphunzitsa kucita zabwino kwa iwo amene awacimwira. Anafunika kugonjetsa coipa ndi cabwino.”

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kumbukurani kuti mphatso ili yonse yomwe Mkristu ali nayo icokera kwa Mulungu kuti aigwiritse. Kodi muidziwa mphatso yanu? Pephani Mulungu kukuthandizani kugwiritsa mphatso pamene mukhala muumoyo wacigonjetso.

THUPI LIMODZI MWA KRISTU

Akristu akhala umoyo waciyanjantso amakhala thupi la Kristu.

Paulo analemba kuti mpingo uli monga thupi la munthu. Thupi ili ndi ziwalo zambiri. Ili ndi maso, makutu, manja ndi minyendo. Thupi lifunika ziwalo zonse ciwalo conse cithandiza. Akristu onse ndi amodzi mwa Kristu. Mpingo unali ndi mamemba ao. Mpingo waukulu uli ndi mamembala 100. Wina 700 mamembala. Gulu liri lonse la Akristu ndi mbali ya thupi la Kristu.

Ngakhale mpingo uli ndi anthu ambiri kapena ang'ono, membala aliyense ayenera kucita nchito. Sitiyenera kuganiza za ife tokha. Tifunika kuthandizana wina ndi mzace. (Onani ndime 3-5) Pamene tigwira nchito pamodzi, tikhoza kucita nchito ya Mulungu. Mulungu apatsa Mkristu aliyense mphatso kugwiritsa pa kumutumikira.

GWIRITSANI PHATSO ZA MULUNGU

Mulungu apatsa Mkristu aliyense mphatso Werengani Aroma 12:6-8. Tiri ndi mphatso izi mu cisomo cace kumanga mpingo. Pamene tigwiritsa mphatso za Mulungu, tithandiza mpingo kukula.

Mulungu anapatsa munthu wina wosapenya mphatso mu Tanzania. Amawerenga Buku Lopatulika ndi manja mu mseu. Iye acitira umboni kwa ma Moslem ndi ena amene sapita ku mpingo. Ngakhale kuti alibe maso munthu uyu acitira umboni kodi ndi mphatso zotani zomwe Mulungu apatsa kwa Akristu? Paulo analemba kunenera (Ndime 6) mphatso iyi ipangitsa munthu kulankhula ndi Mulungu.

Kodi ndi phatso zotani zimene Mulungu apatsa kwa Akristu? Paulo analemba Aroma za mphatso izi.

1. Kunenera (ndime 6) Mphatso iyi ipangitsa munthu kulankhulira Mulungu.
2. Kutumikira (ndime 7) mphatso ipangitsa Akristu kuthandiza omwe ali ndi zosowa. Tiicha kutumikira ena.
3. Kuphunzitsa (ndime 7) mphatso iyi ipangitsa Akristu kuza ena za Mau a Mulungu.

anawapatsa luntha la kuphunzira ndi kukumbukira zomwe anaphunzira, Mulungu anapatsanso Danieli luntha la kunena tanthauzo la maloto ndi maso-mphenya.

Danieli anapambana koposa. Lingaliro lace la kukhala pa coonadi inampangitsa kukhala wolimba.

IYE SANAGWIRIZANE NAO

Mayesero a Danieli sanathe. Kunali kuyamba cabe. Werengani Danieli 6:1-9 kaciwiri. Inenanso za mayesero a cikhulupiriro ca Danieli.

Danieli anali kupemphera masiku onse. Pamene Dariyo anakhala mfumu, anasankha Danieli kukhala otsogolera mu boma lace cimodzi-modzi monga nduna yaikulu ya boma (Prime Minister).

Atsogoleri ena kapena nduna zina sizinakondwere ndi Danieli. Izo zinayetsa kufuna-funa cinthu coipa pa Danieli kuti acotsedwe. Izo zinagonjetsedwa. Potsiliza anaganiza kuti apeze coipa. Danieli anali okhulupirika kwa Mulungu ndi kwa mfumu Dariyo.

Pamene sanapeze coipa kwa Danieli. Iwo anasankha njira ina ya kupembezeramo yatsopano. Anthu onse anafunika kupempha mfumu cinthu ciri conse cimene anafuna. Ngati iwo anafunsa munthu wina ngakhale Mulungu anaponyedwa mu dzenje la mikango. Atsogoleri ena anali okondwa ndi njira imeneyi. Ananena pa iwo oka kodi Danieli adzakhala okhulupirika kwa Mulungu? Danieli anadziwa za lamulo latsopano la Mfumu Dariyo, koma anakana kusiya cikhulupiriro cace mwa Mulungu. Danieli anapitiliza kugwada pa dzenela lace lomwe linali kuyang'ana ku Yerusalemu. Anapemphera kwa Mulungu katatu pa tsiku.

MALAMULO A AMEDI NDI APESIA

Malamulo ao sanali kusinthidwa ngati alembedwa. Atsogoleri aja anapita kwa mfumu ndi kunena za mapemphero a Danieli. Mfumu Dariyo anazindikira kuti analowa mu msampha tsopano, cifukwa anakonda Danieli kwambiri ndipo anamukhulupirira. Mfumu inadziwa kuti ena anali ndi nsanje. Iye sanafune kuponya Danieli mu dzenje la mikango, koma anafunika kutero.

MULUNGU ANAPULUMUTSA DANIELI

Dariyo anaganiza za Danieli usiku wonse. M'mawa mwace, Dariyo anapita ku dzenje la mikango ndipo anamva kufuula kwa Danieli. Danieli anauza mfumu kuti Mulungu anatumiza mngelo yemwe anatseka pa kamwa pa mikango kuti isamukhuze iye. Danieli sanacimwile Mulungu kapena mfumu.

Danieli anapambananso yesero. Anasunga cikhulupiriro cace kwa Mulungu. Anacita cabwino ngakhale ena omzungulira anacimwa.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi mungataye ciani ngati simutaya cikhulupiriro canu mwa Mulungu? Kodi mudzaganiza ciani kwa inu nokha? Kodi mudzakhala ndi abwenzi ambiri? Kodi mudzathandiza anthu kulondola inu? Kodi Mulungu adzavomekeza zomwe mudzacita? Pemphani Mulungu kukuthandizani kukhala okhulupirika kwa iye.

MUTU 11 UMOYO WA CIYANJANITSO

COLINGA: Phunziro ili idzandiphunzitsa za mphatso za Mzimu Woyera ndi momwe zigwiritsidwa.

MAU OYAMBA: Aroma 12

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Aroma 12:1-21.

MAU APAMTIMA: "Musagonje kwa coipa, koma cabwino gonjetsani coipa." Aroma 12:21

Kodi mudziwa pamene mpingo wanu unayambidwa?

Mpingo wina mu Tanzania unayamba mu 1970 pamene anthu awiri anayamba kupembedza mu nyumba. Iwo anali mamembala a mpingo wina kutali.

Kuti ayambe mpingo anapatsa tumapepala tung'ono-tung'ono. Iwo anacitira umboni kwa anthu okwanira 30 a m'mudzi. Iwo analandira Yesu monga Mpulumutsi wao, ndipo anakhala mpingo.

Mpingo unali kukomana sabata liri lonse. Wina anali kalembela pamene wina anali mtsogoleri wa mpingo. Anyamata ndi atsikana ambiri anadzipereka ku nchito ya mpingo.

Aliyense mu mpingo muja anali ndi nchito yocita. Onse sanalalikile, koma onse anagwira nchito. Atsikana, mwacitsanzo anapita kukatunga madzi kutali ku mtsinje. Madzi awa anali kuwaza mu mpingo cifukwa munali pfumbi.

Ena akhoza kudabwa cifukwa cace anthu awiri anayamba mpingo pomwe analibe mbusa kapena munthu wina anapita kumaphunziro. Iwo anakonda Mulungu, ndipo anadziwa kuti akhoza kumudziwa bwino ngati anali ndi mpingo wao mu mudzi.

Paulo anafuna Akristu a ku Roma kuphunzira kukonda Mulungu. Anafuna kuti akhale bwino. Anafuna kuti akhale umoyo wogonjetsedwa. Werengani Aroma 12:1-5 kuti muphunzire tanthauzo la umoyo wacyanjanitso.

Mutatsiliza zonse izi nenani: “Tiyeni tione mu Levitiko 18:5 yomwe ili ndime paulo anali kunena.” Werengani ndime zimenezi. Nenani: “Mose anali kunena za ciyero comwe cinali pa lamulo. Paulo anali kunena kuti ciyero ca cikhulupiriro mwa Yesu Kristu ndiye njira ya umoyo.”

Funsani: Ndani anapita kumwamba ndi kuukitsidwa kwa akufa.? (Kristu).

Nenani: “Sicofunikira kwa munthu kucita zinthu zodabwitsa kuti apulumutsidwe. Kristu anacita zonse zofunikira. Comwe tiyenera kucita ndi kunena kuti ali Mbuye ndi kukhulupirira kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, cabe basi. Mulungu kupyolera mwa Kristu anacita zonse zomwe zinali kufunika kuti munthu apulumutsidwe.

Pemphani kalasi lanu kutsegula ku Aroma 1:33-36. Werengani ndime zimenezi. Nenani:” Ndime izi zinakwaniritsa zonse zomwe Paulo anali kulemba za tanthauzo la cibvumbulutso ca Mulungu kupyolera mwa Kristu. Aoneka monga kuti azindikira kuti mau ace sanali okwanira kumasulira za cibvumbulutso cacikulu coterere. Conco Paulo anangoyamikira Mulungu ndi kuimilira ali kuyanganitsa pa nzeru za Mulungu. Ili monga nyimbo yomwe Paulo anayimba ya ukulu ndi ulemerero wa Mulugu.

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Nenani: “Nyimbo yakuti: ‘His banner over us is love’ inenena kuti ndikukonda ndipo iwe undikonda, koma cacikulu comwe ciri pa ife ndi cikondi. Ndikukonda cifukwa ca Mulungu. Undikonda ca kwa ca Mulungu. Maiko akondana kupyolera mu cikondi ca Mulungu. Ciri ca manyazi masiku ano, cikondi ca Mulungu sicioneka mokwana. Inde timaciona mu mipingo pa sabata, koma kodi timaciona pakati pa masiku? Kodi timaciona pamene atsogoleri a mu maiko amakomana pamodzi? “Kodi ndani ali wofunika kugawa cikondi ca Mulungu kwa aliyense pa dziko? Ndi nchito yathu. Tiyenera kugawa cikondi ca Mulungu ndi aliyense. Kodi ndi anthu angati omwe munagawana nao uthenga wa Yesu? Ndipemphera kuti mudzayamba kugawa cikondi ca Mulungu kwa aliyense.”

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero.

MUTU 3 KWA MPHUNZITSI

COLINGA: Akristu ambiri alephera kuonetsa cikhulupiriro cao. Ndifuna ophunzira anga kuyamba kugwiritsa cikhulupiriro ndi mphamvu.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Mudzagwiritsa mzere omwe tinagwiritsa sabata latha. Ikani pomwe ophunzira anu akhoza kuona. Mutaugwiritsa sabata lino, udzaoneka monga uwu uli munsu.

605 B.C. (Zaka 19)

586 B.C.

Habakuku
adandaula kwa
Mulungu

Yeremiya alembera kwa
akapolo Danieli, Hananiya
Misaeli, Azariya

Mudzagwiritsanso nchito bolodi.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA:

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Buku la Danieli ndi la zinthu zomwe zinacitika pa nthawi yomwe Yeremiya analemba kalata kwa Ayuda. (Onani mutu 2) Mfumu ya ku Babuloni, mfumu Nebukadnezara, anagonjetsa Yerusalemu ndi kutenga anthu kuukapolo. Poyamba anasankha akaswili opanga zinthu okha-okha, ophunzira, ndi a banja la ufumu. Uku ndiko kunali kutengedwa koyamba. Anabweranso ndi kutenga ena. Danieli anatengedwa mu nthawi yoyamba.

Danieli 3-5 itiuza kuti mfumu inaganiza zosankha anyanmata pakati pa akapolo. Anyamata amenewa anasankhidwa kutumikira mfumu. Unali mwambo wa kusankha anyamata pakati pa akapolo kuti akhale okhulupirika kwa mfumu.

Ashipenazi anali woyang'anira wa anchito ace. Anali woyang'anira a banja la cifumu. Iye anaphunzitsanso

anyamata. Anyamata amenewa anali ana kwa mfumu ndiponso alisa ace ndi ana ena a mubanja. Iwo anafunika kukhala anzeru ndiponso a maonekedwe abwino. Cinali cofunika kwa iwo kukaphunzira cilankhulidwe ca ku Babulo kuti atumikile bwino. Zonse za nzeru za ku Babulo zinaphunzitsidwa kwa iwo.

Monga osankhidwa, anyamata a Ciyuda anafunika kudya cakudya ca ku Babulo. Ici cinali cakudya cosayenera cimene ayuda anati cinali codetsedwa.

Ndime 9-10 ionetsa momwe kalembedwe kaciyuda kaonetsa kuti Ayuda anali okonedwa mu dziko pa nthawi ija. Yosefe anakonedwa mu Aigupto, Estere mu nyumba ya Ahasuerus ndi Ezara mu nyumba ya Artexerxers. Danieli ndi nthano inanso yomwe ionetsa kukonedwa ndi mfumu. Mu ndime zapitazo zionetsa anyamata ali kukana cakudya. Mu ndime ya 10 tiona kapolo ali kucita mantha kuti anyamata sadzaoneka anthazi pamaso pa mfumu kopanda cakudya ca mfumu. Ngati iwo adwala iye akanakhala woyimbidwa Mlandu. Ndime 18-19 ndi kutsiliza kwa maphunziro. Anyamata anabweretsedwa pamaso pa mfumu. Anaona kuti aanyamata aja anai anali anthanzi ndiponso opambana mu njira iliyonse. Mutu 6 uonetsa za umoyo wa mtsigolo wa Danieli. Mfumu inakhulupirira kwambiri. Cifukwa ca ici alangizi ena a mfumu anakhala ndi nsanje ndipo anafuna kuti acotsedwe. Iwo anapangitsa mfumu Nebkadnezara lamulo lonena kuti palibe anafunika kupempha kanthu kali konse kwa munthu wina ali yense kupambana kwa mfumu Dariyo kwa masiku khumi.

Danieli 6:10 inena kuti Danieli anapitiliza kupemphera ngakhale pamene lamulo linaperekedwa. Phunziro mu nkhani iyi ndi lakuti, Mulungu adalitsa amene ali okhulupirika kwa iye. Danieli anaponyedwa mu dzenje la mikango cifukwa anaswa lamulo. Mu ndime 21-22 tiphunzira kuti Mulungu analeketsa kuti mikango zisamuonenge pa kutseka pakamwa pa mikango. Ngakhale kuti mfumu inabwera ku dzenje la mikango inapeza kuti Danieli anali mu mtendere pakati pa mikango.

manyazi.” Onse anacimwa, ndiponso onse alandira cipulumutso. Ngakhale Mhelene ali ndi danga lofanana monga Myuda. Palibe kusiyana pamaso pa Mulungu.

Aroma 11:33-36 ili monga nyimbo. Paulo anali kubweretsa maganizo ace onse omwe anali nao pa Kristu omwe anali atalankhulapo mu ndime za mu Aroma. Pena pa nthawi iyi anali kuganiza kuti zonse zomwe anali atanena sizinakwanire. Anafuna kunena zambiri koma anaona kuti sanatero. Ananena kuti palibe cimene tingacite koma kulandila Kristu ndi ku kumulambira. Mau awa ambiri anali a mu Cipangano Cakale ndi kusanganiza ndi maganizo a ci Giriki ndi ci Heberi kuti iwo ayamikire Mulungu bwino.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Funsani: “Kodi ndani akhoza kupulumutsidwa?” Lolani kalasi ilankhuzane. Athandizeni kudziwa kuti aliyense kuli konse akhoza kupulumutsidwa.

Nenani: “Phunzilo lathu lero ndi la cipulumutso comwe cibwera kwa ife pamene tilandira Yesu.”

KUMASULIRA

Nenani: “Lero tidzaphunzira phunziro mu njira yosiyana. Ndidzapatsa yense wa inu pepala ndi pensulo. Ndifuna kuti mutsegule mabuku anu ku Aroma 10:5-13. Pamene upeza ndime izi ndifuna kuti muwerenge kwa inu nokha. Ndipo ndifuna kuti mulembe mafunso omwe mupeza mu ndime zimenezi. Mukhoza kulemba mafunso ambiri monga momwe mufunira.

Patsani kalasi lanu nthawi yokwanira. Ngati mukalasi lanu muli anthu omwe sakhoza kulemba ndi kuwerenga, apatseni wina kuwathandiza yemwe akhoza kuwerenga.

Mukhoza kuyenda yenda mukalasi kuti muthandize. Mukhoza kuthandiza ndi kupanga mafunso. Ndani analemba ndime izi? Kodi citanthauza ciani pa kunena kuti tiyenera kuyesa kucita ciyero? Kodi ciyero comwe ciri pa cikhulupiriro ndi cotani? Kodi tingapulumutsidwe bwanji? Kodi aliyense angapulumutsidwe?

Atatha kulemba mafunso tengani onse. Ndipo werengani mafunso ndipo ophunzira anu afune-fune mayankho.

MUTU 10
KWA MPHUNZITSI

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Ophunzira anga adzamvetsetsa kuti Mulungu afuna anthu onse kupeza cipulumutso ngakhale ali wamtundu wotani.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Pepala ndi pensulo

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA:

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Aroma 10:5-13 Uonetsa kuti Kristu ndiye Mbuye. Pamene Paulo ananena kuti Kristu ndi Mbuye, anamuika pamodzi ndi Mulungu. Liu lakuti mbuye linali lodziwika kwambiri mu nthawi yomwe Paulo analipo. Anacha kaisara mbuye. Ngakhale timilungu ta bodza tinali kuchedwa mbuye. Iyi inali dzina lapamwamba lopambana yomwe munthu akanapatsidwa.

Ku Levitiko 18:5 Kumene Mose ali kulankhula za ciyero cili pa lamulo. Apa Paulo alikunena za kusiyana kwace. -Ciyero comwe ciri pa cikhulupiriro.

“Udzakhala ndi moyo cikhoza kutanthauza kuti udzakhala ndi moyo pa kusunga malamulo.

Paulo anena kuti siciri cothekwa kwa munthu kukwera kuwamba kapena kulowa pansu m'manda kuti apeze cipulumutso. Ici cinacitika kale ndi Yesu.

Comwe cifunika ndi munthu kunena kuti Kristu ndi Mbuye ndi kukhulupirira mu mtima mwace, adzapulumutsidwa. Cikhulupiriro coyamba cinali cakuti kristu “Kristu-mbuye.” Conco pa ciyambi munthu anali kungofunikira kunena kuti Kristu ndi Mbuye. Paulo anena kuti Akristu ayenera kukhulupirira kuti Kristu anagonjetsa imfa. Paulo anali kunena kuti umoyo unafunika kuonetsa cikhulupiriro cimenezi. Ndiye kuti munthu anafunika kuonetsa ndi umoyo wace kuti anali mbali ya banja la Cikristu.

Mu ndime ya 11-13 anaonetsa kuti cipulumutso cinali ca aliyense. “Palibe amene akhulupirira mwa iye adzacinacititsidwa

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Gwiritsani mzere wa nthawi kuyamba maphunziro anu. Funsani ophunzira, “Kodi mukumbukira mzere wa nthawi yanu? Wina amasulire kwa ena zomwe mdzere uonetsa. (Uonetsa cithunzi-thunzi ca zinthu zinacitika.) Lero tidzaonjezera cinthu cina. Cinthu ici cinacita pa nthawi yomwe Yeremiya analemba kalata. Onjezerani 586 B.C. ndi Danieli, Hananiya, Azariya, Mishaeli ku mdzere wa nthawi monga uli mu zothandizira pa kuphunzitsa.”

Pitiliza, “Phunziro lathu lero iphunzitsa kuti tiyenera kusunga cikhulupiriro cathu kukhala colimba. Pamene tigwiritsa cikhulupiriro cathu cimakhala colimba. Anyamata amene tidzaphunzira lero, anagwiritsa cikhulupiriro cao mwa Mulungu, ndipo analimbikitsidwa.

KUMASULIRA

Pemphani ophunzira anu kutsegula mabuku ao ku Danieli 1. Nenani, “Tikhoza kudziwa nkhani mu phunziro lathu lero. Tidzaona zomwe tidziwa. Ophunzira awerenge ndime 3-5. Pemphani wina kuwerenga zomwe zinacitika. Adzafunika kuyang’ana ku ndime 1 ndi 2 kupedza zomwe zinacitika. Onani kuti kalasi lamvetsetsa kuti kunali kutengedwa koyamba. Masulirani kuti Ayuda onse sanatengedwe pa nthawi yoyamba. Ganizirani ndi ophunzira anu kuti Yerusalemu anali kulamuliridwa ndi mafumu oipa. Habakuku anafunsa Mulungu kuti zidzacinacitika liti. Mulungu anayankha kuti Babulo adzawagonjetsa. Ici cinacitika ndipo anthu anatengedwa mu magawo-magawo.

Wina awerenge ndime ya 9-10. Nenani nciani cinacitika pakati pa ndime ya 11 ndi 18? Ndipo funsani: Kodi tidzaphunzira ciani mu nthano iyi? (Kuti anyamata anali okhulupirika pa nthawi yomwe inali yobvuta kukhala okhulupirika.)

Nenani “Zaka zambiri mtsogolo mwace pamene Danieli anakhala mkulu, anapatsidwanso danga ya kuyesa cikhulupiriro cace. Anali atakhala mthandizi wa mfumu. Mfumu Nebukadnezara anali atafa, ndipo mfumu Dariyo anali atatenga ufumu. Mfumu Dariyo anakonda Danieli kwambiri ndi kumukhulupirira kupambana ena onse. Iwo

anakhala ndi nsanje ndipo anafuna kumupha. Kodi iwo anacita ciani? Ophunzira adzapeza yankho mu Daniel 6. Atatha kunena za lamulo, funsani: "Kodi ndi kusiyana kotani komwe lamulo likanacita kwa Danieli ? (Anafunika kusankha pakati pa Mulungu ndi mfumu)

Pemphani ophunzira kuwerenga ndime ya 10. Funsani kodi Danieli anali wokhulupirika kwa Mulungu?" Atatha kuyankha funsani "Kodi ici cinali cobvuta kwa Danieli kucicita? lolani ophunzira alankhuzane pa nthawi yocepa. Funsani kodi cilango ca Danieli cinali cotani?"

Ophunzira awerenge ndime 21-22. Funsani Kodi cinacitika kwa Danieli ndi ciani? Atatha kuyankha funsani, "Kodi anali mtendere usiku wonse mu dzenje? ndipo funsani, "Kodi ndani anabvutika mu mtima? (Dariyo) Nenani: Danieli anaonetsanso kukhala wokhulupirika kwa Mulungu. Ndipo cikhulupiriro cace cinampangitsa kukhala wolimba.

Lembani mdandanda uwu pa bolodi kapena pa pepala:

Danieli akanamvera lamulo la mfumu.

Anyamata akanadya cakudya ca mfumu.

Anyamata Aciyuda asankhidwa.

Mfumu Nebukadneзара aganiza kusankha anyamata.

Danieli apemphera kwa Mulungu.

Woyang'anira apempha anyamata kudya cakudya ca mfumu.

Anyamata anakhala anthanzi kupambana ena.

Danieli agona usiku wonse mu dzenje la mikango.

Mfumu inampeza Danieli ali bwino.

Uzani wophunzira anu kuti zinthu izi sizili mndandanda wabwino. Monga kubwezera kwa phunziro, adzafunika kuika izi mu mndandanda monga momwe zinacitikila.

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani: "Kodi phunziro lathu litiphunzitsa ciani pa njira yomwe tiyenera kukhaliramo? Alofeni alankhuzane.

NYIMBO YA CIYAMIKO

Pamene Paulo analemba za Cikondi ca Mulungu ndi nzeru, mtima wace unali wodzala. Ndime za Aroma 11:3-36 ziri monga nyimbo.

Paulo anayamika Mulungu monga momwe aliri, wabwino, wanzeru ndipo wolemera. Anayamika cifukwa ca mphoto yace.

Munthu anali wocimwa. Munthu anali mdani wa Mulungu. Koma Mulungu anapatsa mphatso ya mwana wace Yesu. Munthu nthawi zambiri sacita bwino kwa ena. Anthu ena amada ena cifukwa cakuti ali osiyana ndi iwo. Samakhala nao bwino cifukwa cakuti ali osiyana ndi iwo. Koma Mulungu sacita ici kwa munthu. Njira za Mulungu zipambana za munthu. Kodi tingauze Mulungu zoti acite? Ai! Kodi anthu ife tingapatse Mulungu comkodweretsa ? Ai! Iye ndi wamuyaya, wamphamvu wodziwa zonse. Kodi tikhoza kumpatsa ciani comwe iye alibe? Iye ndi mlengi wa zonse. Koma anasankha kutipatsa mwana wace. Werengani ndime 35-36, sitikhoza kupatsa Mulungu kupambana zomwe atipatsa. Koma tikhoza kuzipereka tokha. Tikhoza kulola Mulungu kutigwiritsa nchito. Tingaonetse cikondi ca Mulungu kwa ena kupyolera mwa ife.

COMWE CITANTHAUA KWA INE

Yesu ali pafupi nthawi zonse. Tingamkhulupilire ndipo adzatipatsa mphamvu ndi moyo. Kodi muli okondwa cifukwa Yesu akukondani? Uzani wina cikondwerero canu. Kodi mumada ena omwe simufanana nao? Kodi ncifukwa nciani? Ndi Mulungu yemwe anawapanga. Kodi mumada anthu omwe ali ndi katundu wambiri? Ncifukwa ciani? Ndi Mulungu yemwe apatsa anthu zonse zomwe ali nazo. Mulungu adzawerengera aliyense zomwe acita. Kodi muli kugwiritsa bwanji zinthu zimene Mulungu anakupatsani? Kodi muli kuzigwiritsa nchito kuulemerero wace?

Werengani ndime 5 kaciwiri. Comwe citanthauza kusunga lamulo. Ngati munthu akhala oyera ndi lamulo, ayenera kumvera yonse, ndipo palibe angacite ici. Ayuda analephera kukhala olungama ndi Mulungu. Iwo anayesamira pa lamulo kuti liwapulumutse.

CILUNGAMO CA CIKHULUPIIRO

Werengani ndime 6-7. Anthu sanafunike kuyesa kubweretsa Kristu pansu kucokera kumwamba. Anali mziko lapansi. Sanafunike ku mufuna ku malo a anthu akufa. Mulungu anamuukitsa kwa akufa. Ngati anaika cipulumutso pakukhulupirira Yesu sanafunike kumufuna-funa cinali pafupi ndi iwo.

LAPANI NDI KUKHULUPIRIRA

Anthu ambiri akhulupirira ndime 9 monga acikhulupiro a mpingo woyamba. Munthu anafunika kulapa kuti akhale membala. Munthu ananena kuti Kristu ndi Mbuye wace, ndipo ici cikanaonetsa imfa ya Yesu. Ici cinampulumutsa.

Munthu aonetsa kuti cikhulupiro cace ciri mu mtima mwace pamene anena kuti yesu ndi Mpulumutsi wace. Anena kuti apulumutsidwa kucokera nthawi imeneyo. Cinena kuti ndi Ambuye ali ku mbali yace. Sali ndi manyazi kuti ndi Mkristu.

Ngati ici ncoona, ncifukwa ninji tiona Akristu ambiri ali kumva manyazi? Kodi ncifukwa cakuti siali Akristu zoonna.

AYUDA NDI AHELENE

Mulungu anakonda Ayuda. Awakondabe ngakhale lero. Ayuda ndi anthu a Mulungu osankhidwa kalero. Mulungu anawapatsa malonjezo apadela. Koma sitipulumutsidwa mu cifukwa ca momwe tiriri. Cipulumutso cathu ciri pa zomwe tikhulupirira za Yesu. Munthu sapulumutsidwa mu njira ili yonse. Tipulumutsidwa mwa cikhulupiro mwa Yesu.

Ambuye adzapatsa onse cuma, ndipo adzapulumutsa yense wa kuitana dzina lace. Ndani angakhale ndi cikhulupiro. Aliyense wa kutana dzina lace.

Funsani, “Kodi cikhulupiro cathu ticigwiritsa motani? (Pa kucitira umboni kwa ena, kupita ku mpingo, kuphunzira Buku Lopatulika, kuphunzitsa ena.)

Nenani: “Ndifuna inu kucita ici sabata lino.”

Tsekani ndi pemphero.

MUTU 4
KUSUNGIDWA NDI CIKHULUPIRIRO

COLINGA: Phunziro ili indiphunzitsa kuti ndisataye cikhulupiriro.

MAU OYAMBA: Yeremiya 32; Ezra 1.

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Yeremiya 32:6-11, Ezra 1:1-4

MAU APAMTIMA: *“Ndipo anathirana mang’ombe kulemekeza ndi kuyamika Yehova, ndi pakuti ndiye wabwino, pakuti cifundo cace...”* Ezra 3:11

Petro anapita mu nthawi yobvuta mu umoyo wace. Anali ndi matenda a cifuwa ca T.B. Adotolo anamuza kuti anali cabe ndi miyezi itatu yokhala pa dziko cifukwa pwa-pwa wace unaola. Petro anaona komwe umoyo wace udzapita. Kodi monga munthu wokhulupirira anacita ciani pamene adotolo anamuza izi? Kodi muganiza kuti anagonjera?

Ai! cikhulupiriro cace ndi ciyembekezo mwa Ambuye cinamsunga. Miyezi itatu inapita ndipo anali akali ndi moyo. Ndipo anakhala kwa zaka zitatu. Tonse ife timakomana ndi nthawi zobvuta. Mabvuto a dziko ndiponso mabvuto athu amatipangitsa kutaya mtima. Kodi tingacite ciani ngati anzathu ataya ciyembekezo? Tikhoza kuonetsa kuti ife tikali ndi ciyembekezo.

NTHAWI YA MABVUTO A YUDA

Yeremiya anali ndi moyo pa nthawi yomwe Yuda anali m’mbavuto. Nebukadinezara wa ku Babuloni anaukira Yerusalemu. Anatenga golide mu kacisi. Anatenganso anthu a ku Yuda monga akapolo. Iye anauza Zedekiya kuti aika Yeremiya mndende, cifukwa ananena coona.

Mneneri ananena kuti Yerusalemu adzagwa Zedekiya adzatengedwa ndi kuperekedwa ku Yerusalemu komwe iye adzasungidwa. Ahebri adzamenyana ndi Babuloni, koma sadzawangonjetsa. Pa nthawi imeneyo Yeremiya anali ndi uthenga” (Yeremiya 32:1).

MUTU 10
AMODZI PANSI PA MULUNGU

COLINGA: Phunziro ili idzandiphunzitsa kudziwa kuti anthu onse akhoza kupulumutsidwa.

MAU OYAMBA: Aroma 10:1-15; 11

NDIME ZA MPHUZIRO YA LERO: Aroma 10:5-13, 11:33-36

MAU APAMTIMA: “Pakuti palibe kusiyana pakati pa Myuda ndi Mhelene...” Aroma 10:12

Ciyanjano pakati pa mitundu yosiyana ndi bvuto lakale. Cinapangitsa ndeu, nyumba kupwanyika ngakhale nkondo. Kale-kale Ayuda anali kuganiza kuti Mulungu sanade Ahelene, cifukwa sanali Ayuda. Uko kunali kulakwa. Posacedwa apa, Akristu ena anali kuyimba nyimbo. “His banner over me is love” Mtsikana wa Ciyuda anali kuyimba kumeneko kunali mitundu yosiyana-siyana, mu America, (Akuda ndi oyera) a Britishi, Irish, Acikuda, Kikuyu-Wakamba, Jaluo, Meru, Wanyakyusa, Wasambaa, Zambians, Amwenye, ma Arabu onse anali kuyimba. Ndi codabwitsa ca Mulungu kuti anthu onse a mitundu yosiyana akhoza kubwera pamodzi, ali otetedzedwa pansi pa cikondi ca Mulungu.

Ayuda anali ndi bvuto. Sanakonde Ayuda. Paulo anaphunzira kuti Mulungu anakonda Ahelene. Paulo analemba mpingo wa ku Roma. Anafuna kuti iwo adziwe kuti Mulungu anakonda anthu onse kopanda sankho. Anafuna kuti anthu onse akhale olungama ndi Mulungu.

CIYERO CA LAMULO

Werengani Aroma 10:1-13, Paulo anaonetsa Aroma 10:1-4, Muone anafunira abale ace a Ciyuda kupulumutsidwa. Koma anati kwa Ayuda kuti sakanakhoza kupata ciyero pa kuvera malamulo. “Ciyero” citanthauza kuimilira bwino ndi Mulungu. Ayuda anayesa kukhala olungama. Anaganiza kuti akanakhoza kukhala oyera mu mphamvu yao. Anaganiza kuti Paulo ananena kuti akanakhoza kupata kuyera.

Nenani: “Phunziro lathu lero linali la ciyembekezo ndi mabvuto. Latiuza momwe tiyenera kucitira pamene mabvuto abwera. Tiyeni titsilizze mau omwe ali pa bolodi. Tengani nthawi ndi ophunzira anu kunena za m’meme Mkristu wokula acitira, ndiponso m’mene Mkristu wakhanda acitira. Mndandanda wanu udzaoneka monga tere:

Pamene mabvuto abwera:

Mkristu Wokulu	Mkristu Wakhanda
Ayamikira Mulungu	Adandaula
Apilira	Adandaula
Ayembekeza	Alila
Ali oleza mtima	Anena Mulungu
Apemphera	Anena ena
Apeza zabwino mwa izo	Asiya kupita kumpingo
Alandira zonse	Acita ndeu
Ayimba	Alila lila

Lolani kuti mndandanda wanu ukule pamene ophunzira anu ali kuonjezera. Mutatsiliza, funsani: “Kodi inu ndinu yani, Mkristu wokula, kapena Mkristu wakhanda? Tiyenera kuyesa kukomana ndi mayesero ndi kuleza mtima, cipiliro, ndi ciyembekezo. Tiyenei tipemphere.”

UTHENGA WA MULUNGU

Yeremiya analandira uthenga kucokera kwa Mulungu kugula malo ena pamene anali mundende. Anthu sanali kugula malo mu nthawi ya mabvuto otere. Iwo anali kugula pamene anadziwa kuti akanakhoza kulipila. Iwo anafuna kugwiritsa nchito kuzithandiza. Koma Yeremiya anali mundende, ndipo Yuda anali kulamulila ndi Yuda. Koma kodi ncifukwa ciani akanagula malowo?

Mulungu anauza Yeremiya kuti mbale wace Hanamele adzabwera ndi kupempha iye kugula malo ace. Kodi uthenga wa Mulungu unathandiza bwanji Yeremiya ndi Ahebri ena? Kodi Yeremiya anakhulupirira Mulungu. Anakhulupirira kuti adzakwaniritsa zomwe ananena. Uthenga wa Mulungu unalimbikitsa Yeremiya. Mulungu anaonetsa Yeremiya kuti anali akali ndi colinga pa Yuda. Mneneri uja anagula malo aja kwa Mbale wace.

MULUNGU ANAPATSA ZIFUKWA ZA CIYEMBEKEZO

Zaka zinapitapo, Yeremiya anafa ndipo anthu anakhala mu Babuloni. Anamanga nyumba, nayamba malonda. Koma sanaiwale Yuda ndi Yerusalemu. Ambiri a iwo anafunabe kupita ku nyumba. Mulungu anasungabe cikhulupiriro çao.

CIYEMBEKEZO CA YEREMIYA CIZIWIKA

Werengani Ezra 1:1-4 kaciwiri. Sila wa ku Pesiya anagonjetsa Babulo. Mulungu anagwiritsa nchito Sila mfumu yosapembedza. Mulungu anabvundula mzimu wa Sila. Sila anaika lamulo, nailemba kuti ilalikiidwe dziko lonse. “Atero Koresi mfumu yaku Perisiya, Yehova Mulungu wa m’mwamba anadipatsa maufumu onse apa dziko lapansi, nandilangiza nandimangira nyumba mu Yerusalemu ndi myuda. Ali yense wa inu a anthu ace onse, Mulungu wace akhale naye, akwere kunkha ku Yerusalemu...” (Ezra 1:2-3)

Sila ananena kuti Ayuda onse amene sanapite apereke ndalama monga copereka kuthandiza ena. Ayuda mu Babulo anayenera kulipira ndalama za ulendo, cakudya kuthandiza zinthu zofunikira. Anafunika kuperekanso copereka ca kacisi.

Anthu mokondwa anabwerera ku Yuda. Sananyamule mafano kapena milungu ina. Iwo anabwerera kukamanganso

kacisi ya Mulungu wao. Iwo anafuna kupembedza Mulungu mu Yerusalemu. Mulungu anawadalitsa posataya ciyembekezo.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Nainunso mukhale mu nthawi ya mabvuto. Anthu ambiri alibe zinchito. Anthu ambiri ali odwala, osowa bwenzi ndiponso anjala. Mumapeza anthu pafupi ndi inu omwe ali ndi zosowa. Kodi mukhoza kucita ciani kuti muthandize? Mukhoza kukhala abwenzi, ndi kuthandiza. Kupambana zonse onetsani ciyembekezo canu mwa Yesu Kristu. Uzani anthu za Yesu kuti naonso akhale ndi ciyembekezo.

KUMASULIRA

Pemphani kalasi lanu kutsegula mabulu ao mu Aroma 8:18. Werengani ndime zimenezi mokweza. Nenani: "Paulo anena kuti mabvuto omwe tikomana nao pa nthawi ino sangafanane ndi ulemelero omwe tidzakomana nao mtsogolo. Nthawi zambiri pamene tikomana ndi mabvuto timadandaula monga ana ang'ono. Tinali kucita zinthu zambiri koma Mulungu atiyembekezera kukumbukira za mtsogolo. Ngakhale cilengedwe, mitengo, minda, mitsinje zonse ziri kuyembekeza pamene kristu adzabwera mu ulemerero wace. "Genesis 3:17-18 itiuza kuti cilengedwe conse cinasauka pamene munthu anacimwa." Werengani ndime zimenezi. Nenani: "Kutha kwa mabvuto amenewa kudzacitika pamene Kristu adzabwera pa dziko lapansi. Ici ndico ciyembekezo cathu. Aroma 8-25 Itiuza momwe tiyenera kukhalira pamene tiri ndi mabvuto. Kodi tiyenera kukhala motani: (Ndi kuleza mtima ndiponso cipiriro.) Nenani: "Ngati tibvutika ndi kupirira tiri kubvutika monga Akristu okhwima, osati ana ang'ono."

Werengani ndime 26 ndi 27. Nenani, "Ndime ziwiri zabwino izi zitiuza kuti Mzimu Woyera udzatithandiza pamene tipemphera. Kodi atithandiza motani?" (Amamasulira zomwe tifuna kunena kwa Atate.)

Funsani: "Kodi Mzimu Woyera ndani?" (Ndi munthu wacitatu mwa Umulungu.)

Nenani: "Cifukwa ndi Mulungu, akhoza kutidziwa ndi kutimasulira zofuna zathu kwa Mulungu."

Wina awerenge ndime 28-39: "Apa ciyembekezo cathu atimasulira. Mulungu acita zonse kucitira ubwino kwa ana ace. Anatidziwa kale ndiponso anatikonda. Kodi nciani comwe cingatilekanitse ndi cikondi ca Mulungu? (Lolani kalasi linene kuti palibe comwe cingatilekanitse ku cikondi ca Mulungu.)

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Lembani pa bolodi mau awa:

Pamene mabvuto abwera Mkristu wokula,
wakhanda

Mkristu

tikhoza kuuza Mzimu Woyera yemwe adzatipempherera. Adziwa maganizo a Mulungu ndipo akhoza kutiimilira ife. Mulungu nayenso adziwa maganizo a Mzimu ndipo adzamvetsetsa mapemphero ace. Mzimu Woyera ndi Mzimu wa Mulungu, umodzi wa anthu atatu.

Aroma 8:28-29 ndi ndime zabwino zomwe zinyamula ciyembekezo ca Mkristu.

Ndime la 28 itiuza kuti Mulungu acita bwino mu zonse kwa iwo amene akonda. Palibe comwe cicitika kwa ife cimene Mulungu sadziwa.

Ndime la 29 ioneka monga kuti Mulungu asankha kuti ena akhale ace ndiponso ena asakhale ace. Ici sicoona. Cisankho cidalira kwa munthu ndipo Mulungu samulanda. Come Paulo alikunena apa ndi cakuti tidziwe m'mene Mulungu atikondera ndi zomwe atikonzera. Apitiliza kunena ici mu ndime 30. Inena kwa iwo amene abwera kwa ambuye kukhala monga ana ace. Ayenera kukhala monga ana a munthu m'modzi ogawana ulemerero wace.

Ndime 31 kufikira 39 iuza owerenga kuti tiri ku mbali ya Mulungu. Palibe comwe cingacitike kwa ife. Paulo anakumbukira za Abrahamu mu ndime 32 pamene ananena kuti, Mulungu monga (Abrahamu) anali wolola kupatsa mwana wace. Palibe mucilengedwe conse cimene cingatilekanitse ndi Mulungu wathu. Atikonda ngakhale mu mabvuto, mumazunzo, mu cimo liri lonse, mumatenda alionse. Palibe cingatilekanitse ndi cikondi ca Mulungu.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Funsani: “kodi pali wina anabvutikapo mu njira ili yonse? Aloleni anene za nthawi imene anabvutika. Akhoza kunena za matenda kapena imfa ya mbale Wokondedwa, kapena kutaya ndalama, mbvuto mu banja, kupya kwa nyumba, kapena mwana kusowa ndi mabvuto ena.

Pamene aliyense amene afuna atengako mbali, nenani: “Tonse timapita mu nthawi ya mabvuto. Lero tidzawerenga mau acilimbitso yomwe Paulo analemba. Mu phunziro imeneyi tiyenera kuphuzira momwe tiyenera kucitira ngati mabvuto abwera kwa ife.”

MUTU 4 KWA MPHUNZITSI

COLINGA: Ophunzira ayenera kudziwa kuti Mulungu ndi wolimba ndipo athandiza mu mabvuto onse.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Mudzagwiritsa mdzere wa nthawi. Mutaonjezera zocitika izi ku mzere wanu wa nthawi udzaoneka tere:

605 B.C. (Zaka 19)	586 B.C.
Habakuku adandaula kwa Mulungu	Yeremiya alemba kwa akapolo, Danieli Hananiya, Mishaelo Azariya

587 B.C. (Zaka 55)	538 B.C.
Yeremiya mundende	Akapolo abwerera ku Yerusalemu

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Ndime ziwiri, Yeremiya 32:6-11 ndi Ezra 1:1-4, mu phunziro la lero isiyantsidwa ndi zaka zambiri. Cinthu cina cinacitika kwa Yeremiya pa nthawi yomwe Yerusalemu anagwa mu 587 B.C. Nkhani ya Ezra inacitika mu 538 B.C. zaka 55 mtsogolo mwace. Cinthu cacikulu comwe muyera kudziwa ndi cakuti anasiyanitsidwa ndi nthawi. Ndi cofunikira kwambiri mu phunziro iyi, cifukwa mu nkhani ya Yeremiya, ciyembekezo ndi cikhulupiriro mwa Mulungu zinaonedwa kwambiri. Mwa Ezara, ciyembekezo ndi cikhulupiriro zinazindikiridwa.

Mu Yeremiya 32:6-11 tiwerenga kuti Yeremiya anali mndende. Babuloni anali atazingilira mzinda wa Yerusalemu. Yeremiya analandila uthenga kwa Mulungu. Uthenga unati, malo omwe anali a banja la Yeremiya anafuna kugulitsidwa. Malamulo a Ayuda omwe anena za malo kapena munda zipezeka mu Levitiko. Banja inali kuyesa kusunga malo ace ngati nkotheke. Ngati anali kufuna kugulitsa anali kuitana munthu ngakhale wakutali kuti akatenge mundawo, kuti ukhale mbanja. Ici ndico cinacitika mu ndime iyi.

Amalume ace a Yeremiya anali kupita mu nthawi ya mabvuto cifukwa ca zimenezi. Minda tsopano inalibe nchito. Palibe anafuna kugula munda womwe unali pafupi kutengedwa. Koma anthu ambiri anali kuyesa kugulitsa munda yao. Kumbukirani lamulo la mu Levitiko, Salumu, amalume ace a Yeremiya, anatuma mwana wao Hanameli kukauza Yeremiya kuti agule munda kuti ukhalebe mu banja. Yeremiya anagula munda uja ngakhale mu nthawi yotere. Koma kacitidwe kotere kanazindikirika. Yeremiya anali kunena kwa anthu kuti tsiku lina malo ao adzabwezedwa kwa eni ace. Mulungu adzaona kuti adani agonjetsedwa. Sanadandaule kuti ici cidzacicitika pena iye atafa.

Ezara 1:1-4 inacitika Yeremiya atafa. koresi wa ku Peresiya anali atagonjetsa Babuloni. "Tsopano mu caka coyamba ca mfumu Koresi" Sicitanthauza kuti caka coyamba kukhala mfumu wu ku Peresiya, koma caka coyamba ca kukhala mfumu wa Babulo.

Mulungu anagwedeza mtima wa mfumu ya Cihelene. Ici cionetsa mphamvu ya Mulungu kwa Ahelene.

"Mau a Mulungu ndi pakamwa Yeremiya, citanthauza kuti Mulungu adzakwaniritsa cinenero ca Yeremiya, kuti anthu adzabwerere ku Yerusalemu.

Ndime 2-4 inena kuti sila analamula Ayuda onse kuti akabwerera ku Yerusalemu. Conco, Mulungu anacita comwe analonjeza anthu.

MUTU 9 KWA MPHUNZITSI

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kuzindikira kuti akhoza kulandila mabvuto ndi nthawi za masautso mu umoyo wao cifukwa pali nthawi imene mulungu amalimbitsa cikhulupiriro cao.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: COKO NDI BOLODI

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA:

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Aroma 8:18-25 Inena za nthawi ya mtsogolo pamene cimo lomwe ili mu umoyo wa anthu silidzakhala ndi mphamvu. Masautso a nthawi ino ndi zotsatira zace za cimo.

Genesis 3:17-18 inena "...Pakuti wadya za mtengo umene ndinakuuza kuti usadyeko, nthaka ikhale yotembeledwa cifukwa ca iwe."

Pamene munthu anagwa cifukwa ca cimo, cilengedwe conse cinagwa. Ndime izi zitiuza kuti cilengedwe conse ciri kulira cifukwa ca cimo mu dziko. Cithunzi thunzi ndi ca mzimai yemwe ali kubereka ndipo ali mumasautso a akulu.

Koma pali lonjezo lalikulu mu ndime izi, pa nthawi ya mtsogolo pamene Kristu adzabwera mu ulemerero wace, cilengedwe cidzamasulidwa ku ucimo ndi ku zoipa zomwe zipezeka.

Ndime 22 itiuza kuti tiri ndi zipatso zoyamba za Mzimu. Izi zinalandilidwa pa tsiku la pentecoste, ndipo zilandiladwanso pamene muthu alandira Yesu monga Mpulumutsi wace.

Ndime ya 24-25 itiuza kuti ngati tipilira, ciyembekezo cathu cidzakhala coona. Ciyembekezo ndi cakuti Kristu adzabwereradi mu ulemerero ace. Ici ndico ciyembekezo coona.

Ndime 26 ndi 27 ndi ndime zabwino zimene Paulo analemba. Pa nthawi ya mabvuto imene tonse tiyenera kupitamo, tiri ndi Mzimu kutithandiza ife. Pamene sitidziwa kupemphera,

ndani angatiukile?” (Ndime 31) Ngati Mulungu ali kwa ife, ndiye kuti tiri otetezedwa. Tiri ndi ciyembekezo ndi thandizo.

CIPULUMUTSO COTETEDZEDWA

Cikondi ca Mulungu ndi ca mphamvu kupambana cinthu ciri conse mdziko. Mulungu ali kwa ife palibe cingaonoge ife. Ngakhale tisauka ndi kufa sitigonjetsedwa. Satana sangatipambane, Mulungu anapatsa mwana wace Yesu, kulipira macimo athu.

CIGONJETSO COONA

Akristu adzapambana kupyolera mu cikondi ca Kristu. Paulo analemba kuti zinthu zonse izi zigonjetsa mwa iye amene atikonda ife. (Ndime 37) Kodi pali cingatipatule kwa Krsitu? Kodi Paulo ananena ciani mu ndime 37-39? Yamikani Mulungu. Palibe cingatilekanitse ndi Mulungu. Akristu onse ali otetezedwa mu cikondi ca Mulungu.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi nthawi zoipa zimabwera kwa inu? Cikondi ca Mulungu cidzathandiza nthawi zobvutitsa kupanga inu kukhala Akristu abwino. Ngati mukhulupirira Mulungu adzapangitsa mabvuto kucita cina cabwino.

Tikhoza kukhala otetezedwa mwa Yesu cabe. Kodi mwakhulupirira Yesu? Mukhoza kumukhulupirira tsopano. Pemphani Yesu kulowa mu mtima mwanu kuti akupulumutseni ku macimo anu. Ngati mukhulupirira Mulungu tsazalephera.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Funsani kodi munatayapo ciyembekezo pa cintu cina? Lolani ophunzira kulankhuzana. Lolani anene zinthu zomwe zinacitika kwa iwo. Kapena anene cinthu comwe cinacitika mu umoyo wao ndipo anafuna kutaya ciyembekezo. Kumbukirani kuti muli kuphunzitsa akulu-akulu. Iwo akhoza kutenga nkhani ndi kuipereka kwina. Nchito yanu ndi kuona kuti simutaya mutu wa nkhani yanu ya kusunga kapena kutaya ciyembekezo.

Nenani: “Tonsefe timakomana ndi nthawi zobvuta mu umoyo wathu. Timakomana ndi matenda kapena imfa ya okonedwa wathu. Tikhoza kutaya nchito zathu ndi kudwala. Mu nthawi zotere ndi capafupi kuiwala kuti Mulungu ali ndi ife ndipo atithandiza mu nthawi ya mayesero. Phunziro lathu la lero ndi la nthawi yobvutitsa ya Yerusalemu pamene Yeremiya anakana kutaya ciyembekezo.

KUMASULIRA

Lozani ku mdzere wanu wa nthawi ndi kunena kuti: Zinthu zomwe zicitika mu phunziro ili zicitika mosiyana nthawi monga zaka 55. Cinthu coyamba cinacika Yerusalemu asanagwe kwa Babulo. Caciwiri cinacitika pamene Koresi anagonjetsa Babulo ndi kumasula Ayuda omwe anali mu Babulo.

Tidzaika cinthu comaliza pa mdzere wathu. “Lembani caka 538 B. C. ndi kulemba mau, “Akapolo abwerera ku Yerusalemu” Pitolizani: Cinthu coyamba cinacika Habakuku atadandaula kwa Mulungu.” Lozani ku mdzere wanu.

Ophunzira anu atsegule mabuku ao mu Yeremiya 32:6-11 ndi kuwerenga. Gwiritsani nchito mau ali pa kuphunzira koyamba kumasulira za lamulo la Cilevi pa kusunga minda yao m’banja. Nenani: Salamu anafuna kusunga munda wace kuti ukhalebe mbanja. Tiyenera kudziwa kuti Yerusalemu anali ata zunguliridwa ndi Babulo. Palibe yemwe analowa kapena kutuluka mu Yerusalemu. Cinali coonekeratu kuti Yerusalemu adzagwa kwa Babulo. Pa nthawi yotere minda ikhala ilibe nchito ndipo ndalama zikhala zofunika. Pa

nthawi yotere mukhoza kugwiritsa nchito ndalama kuthawa kapena kudyesa banja lanu ndiponso ndi zinthu zina. Munda womwe udzatengedwa ndi ena posacedwa umakhala ulibe nchito. Salamu anaganiza kuti ndalama zinali zofunika kupambana minda. Anaganiza kuti agulitse munda wace kwa wa Cibale, Yeremiya.”

“Pitilizani: Mukhoza kuganiza kuti Yeremiya anali wopusa kugula munda. Ndani angalole kugula munda womwe unali pafupi kutengedwa ndi ena? Koma Yeremiya sanali wopusa. Anali munthu wa Mulungu. Anakhulupirira kuti Mulungu adzabwerezera dziko lao kwa anthu ace. Iye anakana kutaya ciyembekezo ngakhale anali mndende. Yeremiya agula munda uja.”

Pitilizani: Tsopano tidzaona zomwe Mulungu acita. “Ophunzira atsegule ku Ezara 1:1-4. Ndipo awerenge.

Nenani: Mulungu anabwerezera mzinda wa Yerusalemu kwa Ayuda. Ciyembekezo ca Yeremiya cinakwaniritsidwa, ngakhale kuti zinacitika Yeremiya atafa. Mulungu ali okhulupirika kwa anthu ace. Yeremiya sanataye ciyembekezo ndipo Mulungu anampatsa mphoto ya cikhulupiriro cace.

Pitilizani, “Tsopano tiyeni tinene nthano zomwe tinakhala tiri kuphunzira ku masabata anai apitawa. Ndidzayamba nthano pamene ndalekeza ndizaitana wina kupitiliza ndi nthano kufikira titatsiliza.”

Yambani motere: “Habakuku anali munthu yemwe anaganizira za mzinda. Unali kulamuliridwa ndi anthu oipa. Habakuku anaganizira cifukwa cace sanacitepo kanthu pa izi. Imani ndipo pitilizani ndi nthano.

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Nenani: Taona mu mbiri ya Ayuda kuti Mulungu amapatsa mphoto ya cikhulupiriro mwa iye. Tiyenera kukumbukira citsanzo cao pamene tikomana ndi mabvuto kapena mayesero mu umoyo wathu. Citsanzo cao ndi cabwino kwa ife kulondola.”

Tsekani ndi pemphero.

kukhala ndi ciyembekezo, pamene ciyembekezo cathu ciri mwa Mulungu, tiri otetezedwa. Tingakhulupirire Mulungu cifukwa atikonda ife. Mulungu sasintha.

THANDIZO LOLIMBA

Ndime ya 26-27 itiuza kuti Mzimu Woyera utithandiza ife. Kodi muli ndi mphamvu? Kodi muli oleza mtima? Kodi tikhoza kupemphera njira yoyenera? Ai! Koma Mulungu atikonda. Mulungu adziwa momwe timverera. Atumiza Mzimu Woyera kukhala mwa ife kutitsogolera mu umoyo wathu wa Cikristu. Mzimu wace utiuza momwe tikhoza kupempherera. Ngakhale sitiziwa kupemphera. Mzimu Woyera ukhoza kutithandiza.

Kodi ndime 28 inena ciani pa zinthu zabwino. Itiphunzitsa kuti Mulungu akhoza kugwiritsa zinthu zonse kutithandiza ngati tilondola cifuniro cace. Mulungu agwiritsa zomwe zicitika kwa ife kuti tikule mu Cikristu. Ngakhale mabvuto kuti tikule muuzimu.

Paulo anali wolimba. Mau omveka bwino. Tikhoza kuona kuli Mulungu afuna kuti tikule. Sindife olungama, koma Mulungu afuna kuti tikhale Akristu olimba. Afuna kuti tikhale monga Yesu. Mulungu afunika kutithandiza kukula, cifukwa tingakhale monga ana.

Kodi muona momwe ana acitira. Ngati mwana afuna cinthu, amaseka ndi kucita bwino. Ayamba kudandaula ngati sapeza zomwe afuna. Ndipo ayamba kulira, kopanda misozi. Ndipo ayamba kulira misodzi. Ngati zonse izi sizipangitsa kuti apeze zomwe afuna ayamba kumenya makolo ace.

Kwa Akristu ambiri, ici ndi cithunzi-thunzi ca kukula kwa Uzimu. Iwo apemphera. Ayembekeza, koma yankho kulibe. Ayamba kudandaula. Afuna tsopano kulanga Mulungu. Asiya kupita kumpingo. Apitiliza kudandaula. Kacitidwe kotere kaonetsa Akristu otere akali makanda. Mulungu afuna kuti akristu akule kuuzimu. Adzatithandiza kukula. Tiyenera kukula ndi kukhulupirira Mulungu mokwanira.

Mulungu anali ndi colinga asanalenge dziko. (onani ndime 29-31) Mulungu anatikonda kwambiri kuti anapanga dongosolo lace kwa ife. Sitikhoza kudziwa cifukwa cace anatikondera. Koma tikhoza kudziwa cikondi cace. Pamene timukhulupirira atithandiza ife. “Ngati Mulungu ndi wa ife,

MUTU 9

KUSUNGIDWA MU CIKONDI CA MULUNGU

COLINGA: Mulungu akhoza kugwiritsa nchito nthawi zobvutitsa kulimbikitsa cikhulupiriro.

MAU OYAMBA: Aroma 8:18-39

MAU APAMTIMA: “Tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse ziwacitira ubwino...” Aroma 8:28

Zaka zambiri zapitazi kunali namondwe pa nyanja. Bwato lina linamila pa madzi ndipo anthu ambiri anafa. Munthu wina wochedwa Horatio G. Spafford, anataya ana ace onse pa nthawi imeneyi. Pa nthawi ya kulila kwace analemba nyimbo. Nyimbo inanena momwe munthu amverera pa nthawi ya cisoni. Nyimbo iyi ichedwa, “It Is Well With My Soul.” Pena mudziwa nyimbo iyi yakuti ndiri ndi mtendere monga mtsinje ngakhale pamene namondwe atizungulira ife tikhoza kusamira pa mtsinje wa mtendere. Tikhoza kunena kuti zonse ziri bwino. Spafford anali kuuza Akristu kuti Mulungu adzatsamalira ao amene ali ace, ngakhale zobvuta zotani zitabwera.

Aroma 8:18-39 ichedwa “Citetedzo cosatha ca Akristu.” Pamene muwerenga mau lero, funani malonjezo a Mulungu kwa akhulupirira. Malonjezo awa apatsa okhulupirira citetezo. Kodi muli ndi cikhulupiriro cotere?

CIYEMBEKEZO COYERA

Werengani Aroma 8:22-39 dziko lathu ndi lozala ndi mabvuto. Anthu abvutika ndi kufa. Ali a njala ndiponso nkondo. Cilengedwe conse ca Mulungu ciyembekeza dziko labwino. Osati ocimwa okha ndiwo ali ndi mabvuto Akristu naonso ali nao. Cikhulupiriro cao ncolimba ngati zinthu ziyenda bwino. Cikhulupiriro cao cilephera nthawi zina pamene mabvuto abwera.

Tidziwa kuti mabvuto amabwera kwa Akristu. Koma Mzimu wa Mulungu udzadza mitima yathu, kutikumbutsa cikondi ca Mulungu. Tidziwa kuti Mulungu adzatithandiza ife.

Kodi Akristu amacita bwanji pamene mabvuto abwera? Werengani Aroma 8:24-25 mu Buku lanu. Mkristu ayenera

MUTU 5

COFUNIKIRA CATHU KUTI TIYANJANITSIDWE

COLINGA: Ndizaphunzira mu phunziro ili kuti Mulungu andiwerengere macimo anga.

MAU OYAMBA: Aroma 1:16-2:11

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Aroma 1:28-32; 2:1-11

MAU APAMTIMA: “...Onse anacimwa napere...era pa ulemerero wa Mulungu.” Aroma 3:23

Kodi cipulumutso citanthauza ciani? Pena munafunsidwa funso ili nthawi zambiri monga Mkristu, ndi cofunikira kudziwa momwe mungamasulire. Maphunziro otsatira adzakuthandizani kudziwa momwe cipulumutso citanthauza. Maphunziro awa adzakuthandizani kudziwa momwe munthu wopulumutsidwa akhalira.

Aliyense wa ife anakhala wokwiitsana ndi wina. Tinasiya kulankhula ndi iwo. Tinafunika kuyanjanitsidwa. Pamene tinakhala pamodzi ndi kulankhuzana ndipo tinabwera kukumvetsetsa, tinakhalanso abwenzi. Tinayanjanitsidwa.

Kuyanjanitsidwa citanthauza kukhululukira omwe aticimwira ndi kupempha cikhululukiro pamene ticimwira ena. Tikhululukira ndipo tikhalanso abwenzi. Ciyanjantiso cokwaniritsidwa.

Paulo anauza Akristu aku Roma za Ciyanjantiso. Anawauza kuti anthu anafunika kuyanjanitsidwa kwa Mulungu. Iwo anacimwira Mulungu, Ndipo anafunika kukonza zinthu pakati pa iwo. Kodi anthu anacimwira bwanji Mulungu? Kodi anthu akanakhala bwanji abwenzi ndi Mulungu? Ncifukwa nciani anthu afunika kukhala abwenzi ndi Mulungu? Paulo anayankha mayankho onse pamene analemba Akristu aku Akorinto Iye anamva za mabvuto ao a cikhulupiriro ndi mafunso pa cikhulupiriro. Cifukwa iye sanakhoze kupita, anawalemba kalata kuti akawerenge mukacisi.

Paulo anawauza nkhani yabwino ya Yesu, inena za momwe munthu akhoza kukhala bwino ndi Mulungu.

MUNTHU KUUKILA MULUNGU

Werengani Aroma 1:28-32, 2:1-11, Mu Aroma 1:1-27, tiona momwe munthu acokera kwa Mulungu. Ndime 28 ionetsa comwe cicitika kwa munthu. Munthu acimwa pamene acita ici.

Kodi cimo nciani? Cimo ndi kusowa dongosolo la umoyo wathu. Cimo itanthauza kucita coipa. Ndi kuiwala Mulungu. Paulo ananena ndime 28 kuti anthu oipa aiwale Mulungu ndi kuganiza maganizo oipa. Asiya kuganizira za Mulungu. Cimo ipangitsa anthu kucita zoipa.

Munthu anacimwa pamene anacoka kwa Mulungu. Sanakhalenso bwenzi la Mulungu. Mulungu anamulola kucita monga afunira, anasiya kukonda Mulungu. Mu ndime 29-31, Paulo aika mundandanda wa macimo, koma osati onse. Munthu akali kucimwabe mu njira imeneyi pamene acoka kwa Mulungu.

Dyera ndi imodzi ya macimo. Dyera itanthauza kutenga zambiri. Itipatula ife kwa ena. Anthu otere apangitsa Mulungu kukhala wokwiya. Pali zitsanzo za cimo yomwe ipatula anthu ku abwenzi ndi mabanja. Zitsanzo ndi kusamvera ku makolo, ndi anthu ena kutenga cabwino.

ADANI A MULUNGU

Werengani ndime 32 kaciwiri. Paulo ananena kuti munthu akhala oipa ndipo afunika kufa. Munthu ayenera kufa cifukwa ca lamulo. Lamulo linena kuti wochimwa ayenera kufa. Ocimwa amadziwa lamulo imeneyi koma apitilizabe kucimwa. Akhala adani a Mulungu. Anthu amayesa kupagitsa anthu ena kukhala adani a Mulungu. Monga munthu wocimwa amakondwa kuona ena kucimwa naonso. iwo sadandaula ndi cimo. Adziwa cilango ca Mulungu, koma amacimwabe.

MPHOTO YA MULUNGU

Mulungu salandila cimo. Werengani Aroma 2:1-3. Paulo anauza Akristu aci Roma kukhala omasuka ku cimo ndi kukhala bwenzi wa Mulungu.

Funsani: “Ndani yemwe amatithandiza kuti ticite bwino?” (Mzimu Woyera)

Funsani: “Kodi ciyembekezo cathu cokha cimene tiri naco ndi citi?” (Yesu Kristu)

Funsani: “Kodi Yesu angakhoze kutithandiza motani?” Aloleni alankhuzane kwa ka nthawi, ndipo athandizeni kudziwa kuti tiyenera kukukhulupirira Yesu Kristu.

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Funsani: “Kodi ndime izi zikutonthozani?” Ayankhe.

Nenani: “Zinditonthoza cifukwa zindiuza kuti ndiyenera kucita cabwino, koma ndilephera. Ndiri monga munthu mu nthano lomwe taphunzira pa kuyamba kwa phunziro. Koma sitienera kupitiliza kucimwa cifukwa cakuti tikhululukidwa. Tiyenera kukumbukira kucokera kuphunziro latha kuti sitienera kupitiliza kucimwa kuti tipilize kulandira cisomo. Mulungu aletsa. Ife monga Paulo, tidziwa momwe tiyenera kukhalira. Tiyenera kupempha Mzimu Woyera kutitsogolera masiku onse. Tiyenera kupambana cimo nthawi zonse.

Nenani: “Ndifuna kuti tipemphere tsopano. Tisanapemphere ndifuna kuti tiganizire za macimo omwe tiri nao mu umoyo wathu ndi mu mtima mwathu. Ndifuna Mulungu kutionetsa macimo omwe tiri nao obisika. Ndipo ndifuna kuti tiaulule kwa Mulungu wa cete.”

Aloleni apemphere kwa kamphindi kocepa. Ndipo tsekani ndi pemphero ku pempha cikhululukiro.

Anali ndi kasitolo kakangono m'mudzi umenewo. Iye anali kuona zambiri zomwe zinali kucitika mumudzi. Cinthu cimene anakonda kucita ndi kuuza anthu zomwe zinali kucitika mu mudzi. Nthawi zina anali kuonjezera pangono ku zinthu zimene iye anaona. Iye anafuna kuti nthano zace zimveke bwino. Sanali kuonjezera zambiri koma sanali omasuka mu mtima mwace cifukwa anali kudziwa kuti inali boza imene iye anali kunena. Ici cinambvuta kwambiri. Sanakhoze kusiya. Anali odziwika kwambiri mu mudzi ndipo anadziwa ici cinacokera ku nthano zace zimene anali kuwauza.

“Munthu uyu akanchedwa Paulo cifukwa Paulo anali ndi bvuto imodzi-modzi monga ya munthu uyu. Anakonda lamulo koma sankhoze kuisunga.”

KUMASULIRA

Pemphani ophunzira anu kutsegula mabuku ao ku Aroma 7:14.

Nenani: “Mu ndime yathu ya lero, tidzaona mu mtima mwa Paulo. Tidzaona momwe tifanana ndi Paulo.”

Kumbukirani pamodzi ndi ophunzira anu mamasulidwe a mau anai aja omwe munaphunzira sabata latha la cisomo, lamulo, cimo ndi ciyero. Phunziro lathu lero liyamba ndi phunziro la sabata latha. Paulo anena kuti anafuna kucita zabwino koma nthawi zonse anali kucita coipa.”

Werengani Aroma 7:14-8:2. Funsani: “Kodi Paulo anali munthu wotani?” Lankhuzanani. Onani kuti anena kuti Paulo anali munthu monga ife tiliri. Anafuna kucita comwe cinali cabwino koma anali kulephera.

Funsani: “Kodi ncifukwa nciani Paulo anali kulephera kucita cabwino? Lankhuzanani. Lolani kuti apeze mu ndime zomwe zinena kuti inali cimo lomwe inapangitsa kuti acimwe. Funsani: “Pamene tikhala Akristu kodi sitikhoza kucimwa?” Lankhuzanani. Kumbukirani maphunziro a sabata latha kuti mipingo yambiri imaganiza kuti anthu ao siali ocimwa. Thandizani ophunzira anu kudziwa kuti umoyo ndi kuyesa kucita cabwino.

Cimo ipangitsa munthu kukhala kutali ndi Mulungu. Ocimwa adana ndi Mulungu. Mulungu akonda ocimwa ngakhale kuti adana nalo cimo. Ndime 4-5 ionetsa kuti Mulungu ndi wabwino kwa munthu ngakhale pamene acimwa. Mulungu ayesa kuonetsa cimo la munthu. Mulungu afuna kukhala bwenzi ndi munthu.

Mulungu apatsa munthu monga momwe anacitila ngati iye acimwa alangidwa. Ngati munthu akhulupirira mwa Yesu, akhala bwenzi la Mulungu. Lonjezo la Mulungu kwa iye ndi moyo wosatha mwa Yesu. Werengani Aroma 1:16. Ndime iyi inena momwe tingakhalire abwenzi ndi Mulungu. Pamene tikhala ndi cikhulupiriro mwa Yesu tikhala abwenzi ndi Mulungu. Pamene munthu acimwa ndi kuda Mulungu, abvutika, cimo libweretsa cilango cace. Werengani Aroma 6:23 mu Buku Lopatulika. Ndime iyi inena za zotsatira za imfa.

Anthu oipa amene acimwa abvutika. Adzabvutika cifukwa ca cimo lao. Sadzakhala abwenzi a Mulungu.

ABWENZI NDI MULUNGU

Mulungu afuna aliyense kukhala bwenzi lace. Mulungu anapatsa aliyense lonjezo. Anthu onse akhoza kukhulupirira Yesu. Onani ndime 10-11 inena omwe akondweretsa Mulungu. Omwe amkhulupirira ndi kumutumikira amkondweretsa.

Mulungu adzapatsa mtendere kwa onse amene akhulupirira mwa Yesu ndi kumulandira. Ndime 10 inena kuti Mulungu adalitsa omwe amvera iye. Timvera Mulungu coyamba tikhulupirira Yesu Kristu monga Mpulumutsi. Pamene tikhulupirira yesu, tikhala abwenzi ndi Mulungu. Tiyanjani sidwa kwa Mulungu ndipo tikhoza kudziwa cikondi cace kwa ife.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Mulungu afuna kukhala bwenzi wanu. Mulungu safuna kuti abwenzi ace apitilize kucimwa. Kodi ndinu bwenzi wa Mulungu? Ngati ndinu, yesani kuthandiza wina kukhala bwenzi wa Mulungu.

MUTU 5
KWA MPHUNZITSI

COLINGA: Ndifuna ophunzira anga kudziwa kuti munthu aliyense adzawerengedwa macimo ace. Ndifuna kuti alape macimo ao kwa Mulungu.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Palibe.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA::

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Mu Aroma 1:28 kufikira ku 2:11, Paulo mlembi, anena zomwe zicitika kwa munthu amene asiya Mulungu kunjira kwa umoyo wace.

Ndime ya 28 itiuza kuti pamene munthu alephera kudziwa Mulungu, Mulungu adzamusiyira kuti azilambulira iye yekha. Pamene munthu aganzizira za iye yekha, ali kuzilambulira iye yekha. Ali kuzilambila iye yekha. Mulungu amamulola kuti apitilize kuzilambila.

Mu ndime 29 tiyamba mndandanda wa macimo omwe adzadza muthu yemwe asiya mulungu kunjira kwa moyo wace. Pakati pa macimo amenewa pali imodzi yomwe ipambana zonse. Iyi ndi kufuna kucita coipa kwa ena.

Cimo lina ndi kukhumbira, yomwe ipangitsa anthu kucita coipa kwa ena kuti apate. Kucokera ku khalidwe limeneli zina zambiri zikhoza kubadwa.

Cimo lina ndi kusafuna ena kucita zabwino.

Cimo lina ndi lomwe ipangitsa munthu kubvomera cinthu comwe sicili coona. Khalidwe lotere ipangitsa munthu kukhala wasankho. Pali macimo ambiri omwe akhala ochulidwa mu ndime (9-31) Mulungu amada cimo lili lonse.

Aroma 2:1-11 inenedwa kwa Ayuda. Mu ndime zomwe zamasulidwa, Paulo anali kulankhula kwa Ahelene. Tsopano anena kwa anthu ace.

Ayuda anadziwa kuti dziko la Cihelene linali loipa ndi kuti tsiku lina Mulungu adzabwereza anthu atere. Koma Ayuda

kucita cilungamo lamulo labwino ndi kakhalidwe kace komwe kanali ka ucimo.

Mu ndime 1, Paulo apitiliza kumasulira comwe “kugulitsidwa pansa pa lamulo itanthauza mu ndime ya 14 pamene anena kuti anali omangidwa ndi cimo: “...cabwino cimene ndifuna sindicita; koma coipa cimene sindifuna, cimeneco ndicicita.”

Paulo anena za makangano omwe ali nao mu ndime la 16-20 pamene anena kuti abvomekeza ndi lamulo. Anaona kuti anapatsidwa ndi Mulungu, ndipo anafuna kuwalondola. Koma aoneka monga kuti sanakhoze kuziletsa iye yekha. Cimo linamakamiza kucita zoipa. Aka kanali kaonedwe ka Paulo kuti pali zimphamvu zomwe zimamenyana mkati mwa Mkristu.

Kuwawa komwe Paulo apeza pa kukhala ndi zabwino ndi zoipa mwa iye kupangitsa Paulo kunena mu ndime la 21-24 kuti akondwera mwa Ambuye. Afuna kucita bwino umoyo wace wonse. Koma anagwiridwa ndi ucimo ndipo anacita zoipa. “Thupi la imfa” lomwe anafuna kuti acokepo inali thupi lace lomwe inali, la ucimo. Uku sikunena kuti Paulo anada thupi lace. Koma anada cimo.

Paulo anena kuti “Ciyamiko cikhale kwa Mulungu kupyolera mwa Yesu Kristu” Ici ndico ciyembekezo cathu comwe tiri naco kuti tigonjetse dziko. Yesu ndiye yankho. Mu Aroma 8-1-2, Paulo anena za cipulumutso ca Mulungu kupyolera mwa Yesu Kristu. Ndi kupitila mwa Yesu ndi momwe tingakhoze kucotsa imfa mu matupi athu. Ngati tiyenda masiku onse mu Mzimu tiri omasuka ku lamulo la cimo ndi imfa. Tipeza ufulu ku mphamvu ya cimo. Ici cibwera pamene tifuna-funa utsogoleri wa Mzimu woyera masiku onse.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Nenani: “Ndifuna kukuuzani nthano. Kunali munthu wina yemwe anali kukhala mu mudzi wa ung’ono. Bambo m’meneyu anali Mkristu. Anakonda kupita kumpingo ndi kumva uthenga uli kulalidwa. Anakonda kuyimba nyimbo pamodzi ndi anzace. Anakonda kuwerenga Buku lace Lopatulika, ndi kupemphera.

MUTU 8
KWA MPHUNZITSI

COLINGA: Ndifuna ophunzira anu kudziwa kuti monga Akristu, adzafuna cifuno ca kucita cabwino, kupambana kucimwa.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Palibe

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Aroma 7:14-25 ndi ndime yomwe ipangitsa ophunzira kukhala ndi mafunso ambiri. Mafunso awa anabwera kwa Paulo pakulankhula za nchito ya ku uzimu la lamulo.

Paulo alankhula za makangano omwe apeza mu umoyo wace pakati pa mphamvu ziwiri. Zinthu zimene aganiza kuti ziri zoyenera sizitero. Ngakhale pamene adziwa comwe ciri cabwino mu lamulo la Mulungu amamvera mphamvu ya yesero kucimwa.

Popeza tonse tidziwa makangano amenewa ndi cabwino mu umoyo wa Cikristu. Paulo anadziika kwa Akristu atakhala Mkristu, monga muthu wolimba wa Mulungu. Koma atiuza za makangano omwe amapeza mu umoyo wace kuti agonjetse cimo. Mulungu akhoza kugwiritsa umboni wa Paulo kutitonthoza ndi kutilimbikitsa. Paulo alemba za makangano ace ndiponso ayamikira Mulungu yemwe anampulumutsa. Sitili akufa kuucimo titakhala Akristu. Paulo ali kulemba kwa Akorinto, anawauza kuti anali kucita zinthu zomwe anali kucita asanakhale Akristu. Timapitiliza kugonjera ku cimo titakhala Akristu.

Tiyenera kusamira pa Mzimu kutisunga mu njira ya cilungamo. Ndi iye amene adzatitsolera mu njira ya cilungamo ndi yopanda cimo. “Pakuti cabwino cimene ndicifuna, sindicita; koma coipa cimene sindicifuna, cimeneco ndicicita” (ndime 19)

Tiyeni tiyanganitsitse ndime izi.

Ndime 14 itiuza kuti lamulo ndi la uzimu lomwe litanthauza kuti inapatsidwa ndi Mulungu. Paulo analinganiza ciyero,

sanaganize kuti anali pa ciweruzo cimodzi-modzi. Iwo anali kukhulupirira kuti anali ndi ciyanjano ca padela ndi Mulungu. Anali kuganiza kuti Mulungu anakonda Ayuda okha.

Paulo awauza kuti Mulungu nthawi zonse sadzawacitira cifundo, ndi cipiliro. Iwo adzaitanidwa kuyankha macimo omwe acita.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA:

Funsani: Anthu akhulupirira kuti ali Akristu cifukwa anabatizidwa pamene anali ana, kapena cifukwa cakuti makolo ao ali Akristu. Phunziro lathu lero ndi la cimo. Ayuda anakhulupirira kuti sadzaweruzidwa macimo ao cifukwa cakuti anali Ayuda. Masiku ano aliko amodzi-modzi. Ciri cofunikira kwa anthu amenewa kuzindikira kuti adzawerengedwa macimo ao.

KUMASULIRA

Nenani thano iyi: Panali munthu wina wochedwa Yoswa. Yoswa anali kuzikonda kwambiri. Anali kukhala mu nyumba yaikulu. Anali ndi galimoto. M'nyumba mwace munali magesi. Yoswa anakonda kuonetsa zinthu izi zomwe anali nazo.

Yoswa anaonetsanso Cikristu cace. Anali kupita kumpingo Anapereka copereka. Anathandiza kupenta mpingo. Cinthu cimodzi cimene Yoswa anakonda ndi kuitana anthu kunyumba kwace. Anali kutenga nthawi yaitali kuonetsa anthu zomwe anali nazo. Tsiku lina Yoswa anaitana anthu ena kuzadya kunyumba kwace. Anali anthu odziwika mumzinda. Pamene iwo anafika kunyumba kwace, anchito anawalandira ndi kuwapereka ku gome kuti adye. Yoswa sanaoneke. Iye anali wozikonda kwambiri kuti sanaganizire kuti cinali cofunikira kudya nao. Uzani ophunzira kutsegula ku Aroma 1:28. Auzeni awerenge ndime kotsilizira kwa mutu. Atatha kuwerenga, Funsani: “Kodi ndi cimo lotani yomwe Yoswa anali nayo?” “Kalasi lidzabvomekezana kuti Yoswa anacita macimo ambiri. Lidzabvomekezana kuti anacimwa cimo la kunyada.

Funsani: kodi Buku Lopatulika linena ciani pa munthu yemwe ali ndi cimo lotere?

Nenani nthano ili: Marita anali ciwalo ca mpingo. Anali wokhulipirika ku mitsonkhano ya ku mpingo. Nthawi zambiri anali kupezeka ku mpingo. Koma ena sanali kukhala omasuka ngati Marita alipo. Iwo anali kuona kuti nthawi zambiri Marita anali kuwabela.

“Nthawi zina anthu anagula zinthu kwa iye ndi kupeza kuti sizinali zabwino. Nthawi zina anali kupeza kuti aika cinthu cina comwe sicikhala mu pepala yomweyo. “Anthu amenewa anaganizira kuti Marita anali kubela onse anthu. “Tsopano pezani cimo la Marita pa mndandanda. Kalasi likhoza kupeza zambiri

Uzani wina kuwerenga Aroma 2:1-11. Nenani: “Anthu a Ciyuda anali monga Yoswa ndi Marita. Iwo anakhoza kuona macimo a Ahelene koma anaziganizira kuti anali olungama. Anali ndi cijanano capadela ndi Mulungu. Iwo anaganizira kuti cijanano capadela cinawalola kucita ciri conse cimene anafuna. Paulo anawauza kuti analakwa. Ananena kuti munthu aliyense adzawerengedwa macimo ace.

“Iye anapitiliza kunena kuti Ayuda adzakhala oweruzidwa poyamba cifukwa anadziwa Yesu poyamba.”

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Naifenso tiri monga Ayuda. Tiri ndi ucimo mu umoyo wathu. Aroma 3:23 inena kuti onse anacimwa naperewera pa ulemerero wa Mulungu. Tikhoza kuganizira kuti sindife ocimwa, koma sitero. Tikhoza kuona cimo yotizungulira ndiponso ndi kukhala wodabwitsidwa nalo. Tilephera kuona cimo la kunyada mu umoyo wathu. Mulungu atiuza kuti tonse tidzawerengedwa macimo athu. “Ngati ndife Akristu tiyenera kulapa macimo kwa Mulungu monga munthu wotaika acitira. Tiyenera kucita ici masiku onse. Nthawi zina sitikhoza kuona macimo athu. Tiyenera kupempha Mulungu kutionetsa macimo athu. Yohane woyamba 1:9 anena kuti Mulungu ali wolola kutikhululukira macimo athu pamene tipempha kwa iye.”

“Ngati tilola macimo athu kukhala mu umoyo wathu, amatyanjanitsa ku cijanano ndi Mulungu.

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero, kupempha Mulungu kukubvumbulutsirani macimo obisika kwa wina ndi mnzace.

NKHONDO YA MKATI

Werengani ndime 15-16. Kodi Paulo anamvetsa macitidwe ace? Ananena za nkondo ya mkati mwace. Anadziwa zomwe Mulungu anafuna kuti acite, koma sanatero. Paulo anadziwa ciopyezo ca cimo, koma anacimwabe. Kodi ncifukwa nciani? Nciani cinapangitsa kuti amve tere? Kodi ndime 17 ikuti ciani? Paulo anadziwa Yesu. Anakonda Mulungu. Koma umunthu wace siunali wolungama cimo inali mwa iye. Paulo anali womasuka ku cimo, koma sanali wolungama kapena wopanda cimo.

KUKULA MONGA KRISTU

Yesu anali wolungama. Analibe cimo mwa iye. Yesu anacita zokondweretsa Mulungu. Iye sanakwiisepo Mulungu. Ndi citsanzo cathu cagwiro. Tifuna kukondweretsa Mulungu. Ndi tate wathu wa kumwamba.

KRISTU NDI YANKHO

Ndime 14-25 inaonetsa bvuto lalikulu lomwe anthu akomana nalo. Paulo apereka yankho ku bvuto. Werengani Aroma 8:1-2.

Ndime 1 ikhoza kunenedwa mu njira ina: Maganizo akuti munacimwa akhoza kucotsedwa pamene muika cikhulupiro mwa Yesu.

Pamene “tilumikizidwa” ndi Kristu, tisamira pa iye. Mphamvu yace ndi yomwe tifunika. Sitifunika kumenyana ndi cimo tokha.

Pamene tikhulupirira mwa Kristu, Mulungu atipatsa Mzimu Woyera. Umatidzadza ndipo siusiya malo a cimo. Tipeza mphamvu kumenyana ndi cimo ndi kugonjetsa.

Kodi munthu yemwe sali Mkristu akhoza kukhala ndi umoyo wolungama? Ai, akhoza kukhala munthu wabwino, koma munthu wabwino sali wolungama. Koma ngati munthu wabwino uja ndi Mkristu iye adzacimwabe. Yekhayo Kristu akhoza kugonjetsa cimo.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi muli ndi bwenzi yemwe sali Mkristu? Uzani bwenzi lanu momwe akhoza kugonjetsa cimo. Pempherani kuti bwenzi lanu alandire Yesu monga Mbuye ndi Mpulumutsi wace. Ndipo gawanani naye momwe Yesu aliri kwa inu.

MUTU 8
UFULU MWA KRISTU

COLINGA: Phunziro ili idzandithandiza kusamira pa Mulungu ku mphamvu ndi kukula monga Yesu.

MAU OYAMBA: Aroma 7:1-8-17

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Aroma 7:14-25, 8:1-2

MAU APAMTIMA: *"Pakuti onse amene atsogoleredwa ndi Mzimu ndi ana a Mulungu."* Aroma 8:14

Kuli nthano ya munthu yemwe anacedwa kupata ufulu wace. Anakhala zaka makhumi asanu mndende. Anatsiliza nthawi yace ndipo anamasulidwa. Munthu wacikulire uyu analibe acibale kapena abwenzi. Sanadziwe cocita ndi umoyo wace watsopano waufulu. Potsiridza anapita ku ndende.

Akristu ena atsopano ali monga munthu uyu. Anali akapolo ku cimo asanakhale Akristu. Anapata ufulu, koma sanadziwe cocita nao. Anafunika kuphunzira kwa Mulungu. M'malo mwace, anacita zinthu zopweteka Mulungu. Ena anabwerera ku ndende ya ucimo.

Mkristu akhoza kupambana cimo. Mulungu analonjeza Akristu cigonjetso. Paulo analemba kwa Akristu aku Roma za zinthu izi. Werengani Aroma 7:14-25, 8:1-2 kuti mupeze zomwe analemba.

Paulo analemba kuti lamulo linali la uzimu. Paulo ananena kuti anali wa kuthupi. Nayenso anacimwa, ngakhale anaika cikhulupiro cace mwa Yesu.

Nafenso tidzacimwabe, cifukwa sindife olungama. Sitikhoza kukhala olungama monga lamulo. Lamulo litiuza kumvera Mulungu. Cimo litipangitsa kuiwala Mulungu. Cimo ndi lamulo ziri pa nkondo.

Munthu nthawi zonse adzagonjera ku cimo, cifukwa sali olungama. Koma adzaiwala Mulungu ngati akhala pansu pa lamulo. Iye adzalola lamulo kulamulamulira. Aiwala kuti lamulo ndi la kuphunzitsa kakhalidwe, silipulumutsa.

MUTU 6
KUYANJANITSIDWA KUPYOLERA MWA YESU KRISTU

COLINGA: Ndidzaphunzira comwe citanthauza kukhala oyanjanitsidwa ndi Mulungu.

MAU OYAMBA: Aroma 5:1-21

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Aroma 5:1-11

MAU APAMTIMA: *"Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemo..."* Aroma 5:8

Yakobo anakhala Mkristu. Mkazi wace sanali Mkristu. Yakobo anasiya kumwa mowa. Anasiya ndeu. Mkazi wace anakonda kupita kumabawa kukamwa mowa. Mkaziyo anaganiza kusiya mwamuna wace. Mwamuna sanali wokondwa koma anapitiliza kupempherera mkazi wace. Tsiku lina mkazi wace anabwerera ndi kugwada pamaso pa mwamuna wace kuti amumenye, monga mwa mwambo wao. Yakobo anati *"Sindikhoza kukumenya. Ndakukhulukira. Yesu anandikhulukira. Conco, ndakukhulukira."* Anakhala oyanjana pamodzi ndipo nyumba yao inakhala yokondwa.

Munthu afuna kukhala bwenzi ndi munthu. Koma Salandira cimo. Conco Mulungu anacita cinthu cina comwe cinayanjanitsa munthu kwa iye. Werengani ndime izi kuti mupeze comwe anacita.

UMOYO WA MTENDERE

Werengani Aroma 5:1-11. Mu ndime ya 1, Paul anena kuti Mulungu apulumutsa anthu amene akhulupirira mwa Yesu. Munthu anacimwa. Anacoka pamaso pa Mulungu. Koma munthu akhoza kukhala ndi mtendere pamene aika cikhulupiro cace mwa Yesu. Amayanjanitsidwa kwa Mulungu. Kodi mukumbukira tanthauzo la kuyanjana ku mutu woyamba?

Pamene munthu ayanjanitsidwa ndi Mulungu akhala ndi mtendere. Akhalanso ndi mtendere ndi ena. Cikondi ca Mulungu citithandiza kukonda ena.

TIYENI TIKONDWERE

Kristu amapita kwa Mulungu m'malo mwathu, pamene Mulungu atiyajanitsa kwa iye. Mulungu atipatsa cisomo. Cisomo ndi mphatso yaulele. Cisomo cace citipangitsa kukondwera. Timakondwerera za mtsogolo. Pamene Mulungu atikonda tiri ndi ciyembekezo. Tidziwa kuti Mulungu anatipulumutsa.

Tiyenera kukhulupirira kuti Mulungu atikonda. Tiyenera kukhala ndi cikhulupiriro mwa Yesu. Ndipo timapeza cikondi ca Mulungu cosatha ndi kugawana naye ulemerero. (Ndime 2)

PAMENE MABVUTO ABWERA

Mabvuto amabwera kwa aliyense. Umoyo siukhala wosabvuta. Koma pamene tiri a Mulungu, sitikomana ndi mabvuto tokha. Cisomo ca Mulungu citithandiza pamene mabvuto abwera. Tikhoza kukondwera cifukwa cisomo ca Mulungu ciri mwa ife. Tiri ndi ciyembekezo kuti adzatithandiza kukomana ndi mabvuto.

Ndime 3-5 inena kuti tiyenera kukhala okondwa munthawi ya mabvuto. Kodi tiyenera kukhala okondwa cifukwa tiri ndi bvuto? Ai, mabvuto siabwino. Tiyenera kukhala okondwa ndi zomwe tiphunzira mu mabvuto. Mabvuto amapangitsa Akristu kukhala abwino. Mabvoto kwa ocimwa awapangitsa iwo kukhala oipa kupambana. Tiyenera kukondwera kuti cisomo ca Mulungu ciri mwa ife. Atipatsa mphamvu kugonjetsa mabvuto athu. Tikhala abwenzi olimba pamene tipambana mabvuto. (Onani ndime 4) Kuzindikira thandizo la Mulungu ndiponso mphamvu yace.

MPHATSO LA MZIMU WOYERA

Mulungu anapatsa mphatso kwa iwo amene akhulupirira mwa Mwana. Mphatso yomwe anapatsa ndi Mzimu Woyera. Pamene tikhulupirira zooni mwa Yesu, Mulungu atidzaza ndi Mzimu woyera. Atidzaza ndi cikondi cace kupyolera mwa Mzimu woyera. Mzimu woyera utithandiza kukhala monga momwe Mulungu afunila kuti tikhalire.

MPHATSO YA YESU KRISTU

Anthu onse acimwa. Palibe alibe cimo kapena cifukwa. Cifukwa anthu acimwa, afunika kupanga mtendere ndi Mulungu. Afunika kuyanjanitsidwa ndi Mulungu. Munthu sakhoza kuzisintha iye yekha. Anthu ena (Ngati ndidzakhala

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Mipingo yambiri masiku ano akhulupirira kuti sacimwa. Akhulupirira kuti ena acimwa koma iwo sacimwa. Aweruza ena. Pena tiwadiwa anthu otere. Cikhoza kupangitsa ena kusamvera bwino ndipo ena kucoka kumpingo. Tikhoza kuwathandiza iwo pakuzindikira kuti tonse tinacimwa. Paulo anena kuti tisacite kanthu komwe tidziwa kuti kadhakumudwitsa abale ofoka, omwe samvetsetsa kuti onse anacimwa naperewera pa ulemerero wa Mulungu."

Tsekani ndi pemphero.

Nenani: “Phunziro lathu lero ndi labwino. Ndi la cisomo ndi lamulo, ndi la cimo ndi cilungamo. Tisanayambe tione comwe mau awa atanthauza. Nenani: “Liu lakuti ‘cisomo’ imapezeka nthawi zambiri mu Buku Lopatulika. Cisomo cimasulira kakhalidwe ka Mulungu kwa munthu. Ndife ocimwa koma Mulungu atikondabe, alola kutipulumutsa ndi kutinyamula. Cisomo ndi cifuno comwe ambiri atipatsa kupyolera mwa Yesu. Akristu ambiri akonda kanenedwe kakuti “cisomo” ndi cinthu comwe cinapatsidwa mosayembekezera.

Nenani: Monga yagwiritsidwa nchito mu ndime zathu lero zitanthauza malamulo onse a anthu ndi a Mulungu. Nthawi zambiri mu Buku Lopatulika tiwerenga za lamulo, monga lamulo la Cipangano cakale. Nthawi zina, citanthauza kuti Afarisi ndi Alembi ahaonjezera ku malamulo. Koma lamulo mu ndime izi ndi lamulo lonse.”

Funsani: “Kodi cimo nciani?” Apatseni nthawi kuti alankhuzane. Mukhoza kuonjezera macimo ena omwe mwakumbukira.

Potsiliza, funsani: “Kodi cilungamo nciani” Lankhulani pamodzi kufikira mutafika pakubvomekezana kuti cilungamo ndi ubwino. Nenani: “Tsopano pamene tiri ndi matanthauzo a mau anai awa, tiyeni tione ku malemba.”

KUMASULIRA

Nenani: “Tidzaphunzira ndime zonse mu phunziro lathu pamodzi”

Kalasi Lanu litsegule mabuku ao ku Aroma 6:12. Wina awerenge ndime zonse kucokera 12 kufikira 23. Ndipo kugwiritsani nchito mau ali pa kuphunzira koyamba ndi mabuku a ophunzira, bwererani ndi kuphunzira ndime ndi ndime. Zindikirani kuti ndime izi ndi zobvuta ndipo ndi zibvuta kuzimvetsta.

Pamne muli kuphunzira, pitilizani kunenakuti monga AKristu sitifunika kufuna kucimwa koma timacimwa. Musalole ophunzira kuganizira kuti akhoza kukhala opanda kucimwa. Onani kuti amvetsetsa kuti Paulo alikunena za colinga cathu, osati makhalidwe athu.

bwino mu umoyo, ndipo ndidzakhala Mkristu.” Ici sicotheka, Mulungu sanayembekezera munthu kuti akhale bwino. Mulungu sanayembekezere kuti munthu asiye kucimwa. Ngakhale pamene munthu anali kucimwabe Mulungu anapatsa mwana wace kutifera. Yesu anafa m’ malo mwathu. yesu anafa kuti tikhale ndi moyo wosatha.

KODI MUKANATANI?

Mukanafa kuti mupulumutse wina yemwe simunaonepo ngakhale kale lonse. Sicapafupi kufera wina kuti akhale ndi moyo. Yesu anatero! Mu Aroma 5:10, tiwerenga kuti tinali adani a Mulungu, Koma Mulungu anatikondabe. Cifukwa Mulungu anatikonda, analola Yesu kutifera pa mtanda cifukwa macimo athu. Ici ncifukwa cace cionetsa momwe antikondela. Paulo atiuza kuti tikhoza kuyanjanitsidwa ndi Mulungu kupyolera mwa Yesu Kristu. Ngati Yesu akanakana kufa, tikanakhala opanda cikhulupiriro. Yesu anapatsa moyo wace kuti tikhale ndi moyo.

UMOYO WATSOPANO WA AKRISTU

Kodi kunali kutsiliza pamene Yesu anafa? Kodi anafadi? Inde, Yesu anafa. Thupi lace linafa, koma Yesu anaukanso. Yesu sanaferetu. Yesu ali ndi moyo cifukwa Yesu ali ndi moyo, tipulumutsidwa ku macimo athu cifukwa ali ndi moyo, Mulungu atipulumutsa kuucimo wa cimo, ndi kucilango camuyaya. Monga okhulupirika tiri ndi moyo watsopano kupyolera mwa Yesu Mbuye wathu.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Tiyenera kukhala monga Yesu. Umoyo wace utionetsa momwe tingakhaliye. Tinakhulupirira yesu kuti atipulumutse ku cimo. Tsopano tiyenera kumukhulupirira ndi umoyo wathu wamasiku onse. Yesu adzatithandiza kukula mu cikondi masiku onse. Atithandiza kukhala monga iye. Mzimu Woyera, ndi womwe Yesu anatumiza kukhala mu umoyo wathu, ndi kutiphunzitsa kukonda ena. Tsopano ndife abwenzi a Mulungu. Tiyanjanitsidwa ndi Mulungu.

Akristu ayenera kukhala okondwa, kodi ncifukwa ciani? Cifukwa Yesu anatifera ife. Ndife abwenzi a Mulungu. Tiri ndi ciyembekezo ndi cikondwerero cifukwa Yesu anatifera.

MUTU 6
KWA MPHUNZITSI

COLINGA: Ndifuna ophunzira anga kuyanjanitsidwa ndi Mulungu. Ngati ali kale Akristu, ndifuna kuti auze ena momwe anakhalira Akristu.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Ikani mipando kutsogolo kuti mugwiritse nchito pa sowero.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Aroma 5:1-11 Igwirizana ndi ndime yotsiliza ya mutu 4. Liu lakuti "Conco" itenga owerenga kucokera kumalankhulo a cilungamo ku kulungamitsidwa mu mutu 5.

Kulungamitsidwa ndi kacitidwe komwe Mulungu acita mu ciyero. Ndime 1 itiuza kuti tiri olungamitsidwa, tiri ndi mtendere. Mtendere utanthauza cigwirizano ndi Mulungu. Mtendere umenewu uli pamodzi ndi momwe tikhallira. Ndi cifukwa cakuti talandira cilungamo ca kupatsa mwana wace Yesu, ndi pamene tingakhoze kukhala ndi mtendere.

"Ambuye Yesu Kristu" atiuza kuti Yesu ndani. Iye ndi Mbuye wa moyo wathu. Iye ali wolamulira. Timulola kulamulira umoyo wathu. Yesu anali munthu wa mbiri yemwe anthu anakumbukira. Paulo anadziwa zambiri za Yesu. Kristu atiuza kuti ali citsulo comwe Mulungu anagwiritsa nchito kulungamitsa mtundu wa anthu.

"Cisomo" mu ndime 2 ndi cinthu cimene sitinayembekezere kucilandira. Mulungu anatikonda pamene sitinali kumukonda. Anatipulumutsa pamene sitinayembekezere. Tikondwere mu ciyembekezere.

Mu ndime 3-4 pali mau anai ofunikira kwambiri. "Masautso" ndi mazunzo ndi mayesero omwe Akristu akomana nao mu nthawi ino kuti akakhale mu ulemmero mu nthawi zomwe ziri kudza. "Cipiliro" ndi luso la kukwaniritsa kuima, kugwirira, kukana. "Khalidwe" ndi ibweretsa kukhulupirika. Masautso abweretsa cipiliro. Cipiliro cibala khalidwe lomwe ibala "Ciyembekezo." Ici ndico ciyembekezo mwa Mulungu ndi lonjezo lace la moyo wosatha.

Mu ndime la 18, Paulo anenanso kuti tinamasulidwa ku ucimo. Ici sicitanthauza kuti sitidzacamwa, kapena kuti sityetsedwa kucimwa. M'malo mwace tiyenera kutenga ici monga khalidwe la umoyo wa Ckristu mu umoyo wathu. Tiyenera kukhala akapolo aubwino. Kumvetsetsa ici , tiyenera kudziwa kuti kapolo alibe mphamvu iliyonse, ngakhale umoyo wace. Ngati mbuye walamula kanthu kwa kapolo, kapolo ayenera kucita, ndiponso ayenera kucita pamene mbuye wace acifuna. Ngati ndife akapolo acilungamo kapena aubwino, sitidzafuna kucimwa.

Ndime 19 ifanana mumaganizo. Ndife anthu ndipo timvetsetsa monga anthu. Cisomo ndi cilengedwe ca Mulungu, ndipo cipambana kumvetsetsa kwathu Pamene tinali ocimwa tinalola matupi athu kucita zambiri zoipa. Tsopano pakuti ndife Akristu, sitidzafuna matupi athu kucita zoipa.

Ndime la 20 ndi 21 ipitiliza kunena za khalidwe la kapolo ku ucimo. Monga ocimwa, tinakolola za ucimo. Sitinakolole zinthu za ubwino. M'malo mwace mphoto yace ndi imfa.

Ndime 22 inena zomwe anena kale za kumasulidwa ku ucimo. Takhala akapolo kwa Mulungu ndi cilungamo cace. Mu kakhalidwe kotere timapatsidwa mphoto la kuyeretsewa. Ndiye kuti tinaikidwa padela pa colinga ca Mulungu. Cimaliziro ca umoyo wa cilungamo ndi moyo wosatha, uku ndi kunena kuti kulibe cimaliziro ca umoyo wa cilungamo.

Ndime la 23 itiuza kuti pamene ticimwa timalandira imfa. Koma pamene tikhulupirira Yesu tilandira mphoto ya ulele ya moyo wosatha. Sitinafunike moyo wosatha. Mulungu atipatsa kale mwaulere.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA:

Lozani ku funso lomwe mwalemba pa bolodi kapena pa pepala. Funsani: "Monga Akristu kodi tiri omasuka kucimwa, kapena omasuka ku ucimo? Aloleni alankhuzane pang'ono. Ena akhoza kunena kuti sitili omasuka ku ucimo kapena omasuka kucimwa. Bvomerani kuti ici ncoona.

MUTU 7
KWA MPHUNZITSI

COLINGA: “Ciri cofunikira kwa ophunzira anga kudziwa kuti “kukula mwa Kristu” citanthauza ciani kuti azindikire m'mene iye aliri mu ciyanjano cace ndi Kristu.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Lembani pa bolodi kapena pa pepala lalikulu mau awa: “OMASUKA KUCIMWA KAPENA OMASUKA KU UCIMO?”

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA:

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Aroma 6:12-23 ndi mau obvuta kumvetsetsa. Paulo aoneka monga alemba pa mutu umodzi. Ngati tikumbukira kuti iyi ndi kalata osati buku, tikhoza kumvetsetsa bwino buku la Aroma. Paulo alikulemba kalata monga momwe timalemba.

Ndime 12-14 ndi gawo la manenedwe a Paulo pa cimo ndi lamulo. Anena kuti Mkristu sayenera kukhala omasuka ku ucimo cabe, komanso kumasuka ku mphamvu ya mayesero a ucimo. Paulo anena kuti cimo ilipo, ndi kuti tonse timayetsedwa kucimwa, koma sitiyenera kulola cimo kulamulira matupi athu. Tikane mayesero. Pamene ndime la 14 linena kuti cimo ilibe ulamuliro pa Mkristu cifukwa ali pansu pa cisomo, ikutanthauza kuti cimo siliyenera kukhala ndi ulamuliro pa munthu uja. Iye anthu osinthidwa sitiyenera kukhala ndi cifuno ca kukhala ndi cimo mu umoyo wathu.

Mu ndime la 15, atifunsa kuti tiyenera kucimwa cifukwa sitili pansu pa lamulo koma pansu pa cisomo. Ndipo ayankha kuti “Ai.” Tinasiya umoyo wakale. Cikhulupiriro cathu cinaikidwa mwa Kristu. Tinalandira cisomo.

Mu ndime 17, Paulo anenanso kuti tinamasulidwa ku ucimo. Tiyenera kudziikidza ku ciphunzitso catsopano. Ici cikhoza kukhalira kuti onse okhulupirira anali kulangizidwa akalibe kubatizidwa. Munthu wosaphunzitsidwa sakanabatizidwa. Akristu atsopano ali kulangizidwa kuti ayenera kukwaniritsa malamulo ao asanabatizidwe.

“Cikondi ca Mulungu cinathilidwa” monga mvula pa nthaka louma.

Ena amacha ndime 6-11 nyimbo ya cikondi. Ndi cikondi ca Mulungu kwa anthu. Mulungu akonda munthu cifukwa Mulungu ndi Cikondi. Si cifukwa cakuti munthu afunika kukonededwa.

“Pamene tinali ofoka” citanthauza kusakwaniritsa kuzipanga abwino. “Pa nyengo yace yabwino citanthauza kuti Mulungu ali ndi nthawi yace yocitiramo zinthu. “Kristu anafera ocimwa” itiuza kuti Kristu sanafere olungama kapena abwino koma iwo amene sanayembekezere nsembe yotere.

Ndime ya 9 itiuza kuti tikhoza kupulumutsidwa ndi mwazi wace tsopano, koma tiyenera kupulumutsidwa ku mkwiyo wace womwe uli mkudza.

“Ciyanjano” ndi kuzibweretsa mu ciyanjano cabwino ndi Mulungu.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Pemphani wophuzira kuwerenga nthano ya Yakobo kucokera ku buku la ophunzira.

Nenani: “Iyi ndi nthano labwino la ciyanjanitso pakati pa Yakobo ndi mkazi wace. Mulungu afuna kuti tiyanjanitsidwe ndi anzathu. Koma kupambana apa, afuna kuti ife tiyanjanitsidwe kwa iye. Sabata latha tinaphunzira za kufunikira kwathu kwa kuyanjanitsidwa. Phunziro lathu lero litiuza momwe zimakhallira titayanjanitsidwa ndi Mulungu.”

KUMASULIRA

Pemphani ophunzira anu kutsegula mabuku ao ku Aroma 5:1-11. Pemphani wina kuwerenga ndime zomwe tiyenera kumvetsetsa tanthauzo lace. Ndidzalemba mau ndi tanthauzo lace pa Bolodi kapena pa pepala.

Lembani mau awa:

Kulugamitsidwa

Mtendere

Mbuye

Kristu

Yesu

Cisomo

Ciyembekezo

Cimwemwe

Mazunzo

Kupilira

Khalidwe

Cikondi

Kuyanjanitsidwa

Yambani ndi liu lakuti Cilungamo. Mutaillemba pa bolodi, mulole ophunzira kupeza liu lakuti "Kuyanjanitsidwa" mu ndime izi. Athandizeni kudziwa comwe itanthauza. Ayenera kunena kuti: Njira yomwe Mulungu abweretsera anthu ku ubwino.

Pitilizani mu njira imeneyi ndi liu liri lonse. Gwiritsani nchito mau ali pa kuphunzira koyamba kuthandiza kalasi lanu kudziwa tanthauzo la liu. Nthawi zonse lembani tanthauzo pa mbali pa liu.

Pamene mutsiliza, pemphani wina kuwerenganso ndime kugwiritsa nchito tanthauzo zomwe mwapeza.

Kuwerenga kwa ndime yoyamba kuyenera kukhala kotere:

Conco cifukwa Mulungu anatibweretsa ku ubwino, tiri ndi cigwirizano ndi Mulungu kupyolera mwa Yesu wotilamulira."

Pitilizani mu njira imeneyi ndi ndime zonse. Ophunzira anu ayenera kukhala odziwa tsopano ndime zambiri.

KUPULUMUTSIDWA KUTUMIKIRA MULUNGU

Paulo anauza Akristu a ku Roma kuti sanali olimba kuuzimu. Mulungu anakhululukira macimo ao. Anali omasuka cifukwa anakhulupirira Yesu. Sanalinso akapolo ku cimo. Koma Akristu atsopano afunika thandizo kuti amvetsetse zinthu za uzimu. Paulo ananena poyera kuti Akristu sali olungama anacimwa. Paulo analemba momwe Akristu akhoza kukulira. Mkristu wofoka afunika kukula kuti amvetsetse zinthu za uzimu. Mkristu amafuna kucita cilungamo. Ngati akula monga Kristu, adzazipereka yekha kwa Kristu. Ndiye angakhoze kukhala umoyo womwe Mulungu afuna kuti akhalire (Ndime 19)

MPHOTO YA CIMO

Pamene munthu anali mdani wa Mulungu, Mulungu sanakhoze kumulamulira. Anali omasuka kwa Mulungu. Anali omasuka ku umoyo wolungama, koma anali kapolo ku cimo. Kodi cimo itipatsa ciani mu umoyo? Akristu akhoza kukumbikira momwe umoyo wao unaliri asanalandire Yesu. Paulo anafunsa Akristu a ku Roma comwe cimo inawapatsa. Cimo ibweretsa imfa. Pamene tinali akapolo ku cimo, tifunika malipilo. Malipilo ace ndi imfa.

MPHATSO YA MULUNGU

Mphatso sitimaigwirira nchito. Ndi yaulere. Kodi mphatso ya Mulungu kwa ife ndi yotani? Mphatso ya Mulungu ndi moyo wosatha. (Ndime 22-23). Kodi ndi liti pamene Mulungu amatipatsa mphatso yace yaulere? Werengani ndime 23. Mulungu anatipatsa mphatso yace yaulere pamene tinakhulupirira Yesu.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Pamene mulandira Kristu, muyamba umoyo watsopano. Umoyo uyu utanthauza kuti mukule. Kodi muli kukula? Kodi Muli kukula monga Yesu? Pempherani kuti Mulungu akuonetseni momwe mungakulile monga Yesu.

OMASUKA MWA YESU

Pamene ticimwa, tiri kubvomera mbuye wathu. Cimo ndiye mbuye wathu. Iti lamulira ife. Munthu sanalengedwe kuti acimwe. Mulungu analenga munthu kusankha cabwino ndi coipa. Mulungu anafuna kuti munthu asankhe cabwino koma munthu anasankha kucimwa. (Onani ndime 12) Pamene tikhala Akristu, tisiya kumva ucimo.

Nthawi zina cinthu cina kapena munthu akhoza kutiyesa kuti ticimwe. Tikhoza kufuna kucimwa, koma sityenera kugonjera ku cimo. Pamene tinali mu cimo, tinali monga anthu akufa. Tsopano titumikira Mulungu, ndipo tiri amoyo mwa Kristu. Cimo litilesa kutumikira Mulungu. Pamene ticotsa cimo, Mulungu akhoza kutigwiritsa nchito.

OMASUKA KU ULAMULIRO

Cisomo ndi cikondi ca Mulungu ca cikondi. Yesu Kristu anabweretsa cisomo kwa munthu. Cisomo cingatenga malo a lamulo la Mose. Lamulo linafuna ciweruzo, koma Yesu anabweretsa cisomo m'malo mwa lamulo. Sitili pansu pa lamulo. Tikhala pansu pa lamulo. Kodi Mkristu ali ndi ufulu wotani? Cikhulupiriro cathu mwa Yesu citimasula kulamulo. Kodi ici cithanthauza kuti tiri omasuka kucita zonse zomwe tifuna kucita? kodi Paulo ananena ciani? Ananena kuti sityenera kucimwa cifukwa ndife omasuka. Werengani ndime 15 kaciwiri.

KODI MBUYE WANU NDANI?

Mu ndime 10, Paulo anauza Akristu aku Roma kuti anali ndi cisankho. Akanakhoza kusankha kucimwa, kapena Mulungu. Muli ndi cisankho cimodzi-modzi.

Munthu aliyense azisankhira yekha. Cimo litsogolera njira ya ku imfa. Kumvera kutsogolera njira ya ku moyo wosatha. Pamene tisakha Mulungu, tisitha Mbuye. Satana asiya kukhala mbuye wathu, ndipo Mulungu akhala Mbuye wathu.

Pamene tibvala cikhulupiriro mwa Yesu. Akristu amasulidwa kuti akhale ndi umoyo woyera. Umoyo wa Yesu utionetsa njira yabwino yomwe tikhoza kukhalira. Paulo ananena kuti tiyenera kukhala akapolo a ciyero. Mwa Yesu, Mulungu anationetsa njira yoyenera. Werenganinso ndime 18. Lembani pa mbali pa ndime mu Buku Lopatulika. Kodi Mbuye wanu ndani, Mulungu kapena satana?

Nenani: “Kodi muciona codabwitsa kwa Mulungu kuti anafera ocimwa?” Lolani ophunzira kulankhuzana.

Funsani: “Ndani wocimwa?” Aloleni alankuzane. Bvomerani kuti tonse ndife ocimwa, koma kuti ena aife tinapulumsidwa ndi cisomo.

Funsani: “Kodi tiri ndi nchito ya ocimwa amene sanapulumsidwe ndi Mulungu? (Inde tiyenera kugawa uthenga wabwino wa Yesu kwa onse otaika.)

Nenani: Ena aife tigawa cikhulupiriro cathu bwino. Koma ena aife sititero. Simacita tero cifukwa sitidziwa momwe tikhoza kucitira. Lero tidzaphunzira monwe tikhoza kucitira.

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Pangani sowero la kucitira umboni. Pemphani wina kubwera kutsogolo kuyelekeza munthu wotaika. Onani kuti mwasankha Mkristu kucita ici. Akhale pa mpando kutsogolo, inu mukhale pali pa mpando wina. Ndi munthu yemwe abwera nanu kucitira umboni.

Gwiritsani nchito njira yomwe mumacita pakubweretsa wina kwa Ambuye. Njira yosabvuta ichedwa njira ya Aroma. Mudzagwiritsa Aroma 3;23; 6:23; 5:8; 10:9-10; 10:13.

Coyamba, yelekezani kuti mwabwera kunyumba ya munthu wotaika uja. Mpatsemi moni monga momwe mumacitira. Pitilizani ndi nkhani ili yonse kuyembezero danga la kunena nkhani ya Yesu. Mukhoza kufunsa: “Kodi mumapita kuti ku mpingo? Mafunso ena akhoza kukuthandizani kuti mufunse ngati anayanjanitsidwa ndi Mulungu. Ndipo gwiritsani nchito njira ya cipulumutso ndi “munthu wotaika uja.” Ngati abvomera kulandira Yesu pempherani naye pemphero la pafupi. Munena ndipo iya alondola. Pemphero ikhoza kukhala lotere: “Ambuye ndine wocimwa. Ndifuna kukhala Mkristu. Ndifuna kusiya macimo ndi kukhala watsopano mwa Yesu Kristu. Khululukirani macimo anga tsopano. Ambuye ndilandira Yesu monga Mpulumutsi wanga. Ndipemphera mu dzina a Yesu. Amen.

Mutatha sowero, itanani ena kucita naonso. Ngati kalasi lanu ndi lalikulu agaweni mumagalu awiri. Acitire umboni kwa wina ndi mnzace.

(Mpunzitsi, ili ndi phunziro lofunikira kwambiri. Ngati muona kuti simukhoza kuphunzitsa bwino itanani abusa kubwera ndi kucita sowero. Ndi cofunika kuti icitidwe.)

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero. Pemphani Mulungu kupatsa aliyense danga la kucitira umboni sabata lino.

MUTU 7 AMOYO MWA KRISTU

COLINGA: Ndifunika kukula nthawi zonse mu umoyo wanga wa Cikristu. Phunziro ili idzandithandiza kudziwa ngati ndiri kukula.

MAU OYAMBA: Aroma 6

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Aroma 6:12-23

MAU APAMTIMA: *"Comweco, ngati munthu ali mwa Kristu, ali cilengedwe catsopano; zakale zapita taonani, zatsopano zafika."* 2 Akorinto 5:17

Miriamu anali kuphika. Mwana anali kusowera mu nyumba. Anamva madzi ali kutaika ndipo anadziwa kuti mwana anali kusowera ndi madzi mu m'gomo. "Ayi ali bwino" maganizo a Miriamu amenewa.

Patapita nthawi yocepa sanamve mwana ali kusowera ndi madzi. Mwamsanga anapita kukaona. Cacisoni! mwana anali atagwera mu m'gomo ndipo analephera kutuluka, Miriamu anamcotsa. Mwana sanali kupuma. Anayamba kuthamangira kumzinda pamene anali kuthamanga anakomana ndi munthu yemwe anali ndi njinga. Iye anamthandiza kumupereka ku cipatala. M'njira anamva mwana ali kuyamba kupuma. Ku cipatala, adotolo anaona uja mwana bwino-bwino. Anauza Miriamu kuti "ali moyo, sadzafa!" Iyo inali nkhani yabwino.

Aliyense wa ife afunika kukhala wamoyo. Tiri akufa mu ucimo, ngati sitinakhulupirire mwa Yesu. Sitikhoza kukhala mu cinyanjano ndi Mulungu, ngati sitikhulupirira Yesu kutithandiza. Yesu yekhayo ndiye akhoza kutiyanjanitsa.

Pamene tisanakhulupirire Yesu monga Mbuye ndi Mpulumutsi, tinali akapolo ku ucimo akapolo a Satana. Tinaganiza kuti tinali omasuka, koma tinali olamulilidwa ndi satana. Pamene tikhulupirira mwa Yesu, cimo silitilamulira ife. Paulo analembera mpingo wa ku Roma, kuwauza kuti anali omasuka ku cimo. Werengani Aroma 6:12-23 kuphunzira momwe Kristu akhoza kukhalira omasuka.